# *O Ambuye, Kamodzi Kenanso Basi*

Mmawa wabwino, abwenzi, kapena madzulo abwino. Ine ndinaswa wotchi yanga, Ine sindingakhoze kudziwa nthawi yomwe ili. [M'bale akuti, "Ukadali mmawa, m'bale."—Mkonzi]. Ukadali mmawa, sichoncho? Chabwino.

2 Kupatula apo, ife tikukhala mu Muyaya. Ife tiribe nthawi. Malire a nthawi anaima pamene Yesu Khristu anandipatsa ine Moyo Wake mkati mwa ine, kuti ndizikhalira nawo moyo, chotero ndife zolengedwa Zamuyaya pakali pano, tikukhala limodzi mmalo Ammwambamwamba mwa Khristu Yesu. Nthawi yotani!

3 Tsopano ili ndi tsiku langa lachiwiri chabe kuno ndi inu, koma, mai, ziri ngati manyuchi ozizira m'mawa, iwo amakhala owundana komanso odabwitsa. Ine sindinayambe ndamvapo kukoma inemwini kenanso mu msonkhano uliwonse. Ndipo ine ndikumayang'ana pozungulira tsopano, usiku iwo akumakhala odzadzana kwambiri ine ndikumalephera kumuwona aliyense, koma lero ine ndikukhoza kuyang'ana pozungulira. Ine ndinali nawo mwayi wogwirana chanza ndi gulu labwino ili la atumiki mu gulu ili kuno.

4 Ine ndikukumbukira bambo wachikulire ankakonda kubwera ku tchalitchi chathu, dzina lake John Ryan. Eledara Ryan, iwo ankamutcha iye. Iye anali wochokera ku Dowagiac, Michigan. Ndipo iye ankakonda kulalikira pang'ono pokha, ndipo kenako nkuthamangira mmbuyo ndi kudzagwira dzanja langa. Ndiyeno iye amakhoza kulalikira pang'ono pokha, ndi kuthamangira mmbuyo ndi kukagwira dzanja langa. Ine ndinati, "M'bale Ryan, ine—ine ndikuyamikira zimenezo, koma ine—ine sindikupeza tanthauzo la chifukwa chimene inu mumachitira zimenezo."

5 Iye anati, "Pamene batire lafooka, ine ndimafuna kuti ilo ndililichaje, kotero ine ndiye ndimangolichaja ilo lonse."

6 Ine ndangomuwona kumene a—mtumiki wa Methodisti wochokera uko ku dziko langa, yemwe wangolandira kumene Mzimu Woyera, ndipo ndinamubatiza iye. Wakhala cha kuno kumanzere kwanga, M'bale Junior Jackson. Ine ndinamuwona iye akugwedeza manja ake monga choncho, anakhala ngati wandikumbutsa ine za M'bale Ryan. Ndi angati akuganiza kuti Amethodisti sangakhoze kulandira Mzimu Woyera? Inu mukulakwitsa. Imiririrani, M'bale Junior Jackson, iye ndi mkazi

wake wokondedwa pamenepo. Iwo ndi ochokera kumusi mu Indiana uko, mtumiki wa Methodisti.

7 Ali kuti Willard Collins? Kodi iye ali mchipinda muno mmawa uno? Kodi inu muli pati, M'bale Willard? Ine ndimaganiza kuti iye anali pozungulira kuno. Mtumiki wina wa Methodisti waima cha kuno, ngati inu simukuganiza kuti Amethodisti akhoza kulandira Mzimu Woyera ndi kudzabatizidwanso. Imirirani, M'bale Collins. Ndi ameneyo mmodzi wina. M'bale anali uko ku Asbury Koleji ku Wilmore, Kentucky, kuchokera ku maziko a mbiri yabwino a Methodisti.

8 Tsopano pali anthu ena ambiri amene ali ndi ine pano, amene—amene abwera kuno. Ine ndinawamva iwo akuti "ameni," ndipo ine ndikudziwa iwo ali pano, koma ine sindikutha kuwawona iwo. M'bale Fred Sothmann wochokera ku kachisi ku Jeffersonville. Fred, kodi iwe ndi M'bale Tom muli muno? Ine ndikukhulupirira ine ndikumumva iye akuti, "Pano." Cha kuno pa ngodya, eya.

9 Ndife okondwa kwambiri kukusonyezani amuna awa. Ine sindikuwona ndendende pa nthawi ino, mwina alipo ena pano amene ine sindikuwadziwa. Ine ndikuganiza M'bale Jack Moore wangotsiriza kuyankhula. Ndipo—ndipo chotero awa ndi amuna abwino, ndipo ife timawakonda iwo.

10 Ndipo tsopano yakhala nthawi yodabwitsa chotero ya kudzakhala pano. Ine ndinati kwa iye, "Mkazanga," mkazi wanga, ine ndinati, "iwe—iwe umayenera ukanabwera mu msonkhano uwu." Ife timakhulupirira mu msonkhano wabwino wachikale wa chipentekoste. Ife timakhulupirira, kuti kumene kuli ufulu mu Mzimu wa Mulungu, kuti magawo onse osiyanasiyana a zipembedzo akhoza kubwera pamodzi ndi kudzakhala limodzi mmalo Ammwambamwamba, ngati mpingo. Kusiyana kwathu sikupanga kusiyana kulikonse kumeneko, pamene tikhala mwa Khristu, ife timakhala pansi pa Magazi ndi mu chiyanjano cha chikondi Chake.

11 Ndipo ine ndikufuna kuti ndinene izi kwa gulu ili la atumiki. Ine—ine ndinabwera mu Pentekoste kuchokera ku Missionary Baptist, ndipo ine ndimayamikira Pentekoste. Iwo ndi anthu anga. Ine ndimawakonda iwo. Ngati ine ndikanaganiza kuti ulipo mpingo uliwonse wolondola kuposa umenewo, ine ndikanakhala ku mpingo winawo. Koma ine ndiri ndi Pentekoste, chifukwa ine ndikuganiza kuti ndi chinthu chapafupi kwambiri chimene ine ndimachiwona ku Lemba. Ngati ine ndikanadziwa chinachakenso, ine ndikanakhala ndi iwo; ndipo chotero, osati kunyozetsa chikhulupiriro china chirichonse, osati nkomwe. Koma chifukwa chimene ine ndimaganizira za Pentekoste, chifukwa ndi pafupi ndi chimene ine ndikuganiza ndi cha Mwamalemba, kuposa chirichonse chimene ine ndikuchidziwa.

12 Ndipo pali chinthu chimodzi chodziwika mu msonkhano waukulu uno, chimene ine ndachizindikira, ndicho, akazi a nkhope-zoyera; palibe za zodzipenta zimenezo, inu mukudzidwa, kapena chirichonse chimene inu mumachitchula zinthu zimenezo. Ine sindimazikonda zimenezo. Zimenezo si zoyenera kwa Akhristu. Huh-uh. Uko nkulondola. Ine—ine ndimazikonda zimenezo. Ndine wa sukulu yachikale imene imakonda chiyero, inu mukuona. Ine ndimakonda kuwawona akazi . . . Inu mukudziwa, ine sindikutanthauza . . .

13 Ano si malo onena chirichonse, nthabwala ndi kusinjirira, kumanena chomwecho. Koma ine sindikunena izi mwa tanthauzo limenelo. Ano si malo a zimenezo.

14 Tiri pomwepo, ndi liti pamene inu nonse munapeza chinthu ichi? Ichi chinabwera kuchokera ku kachisi wanga, izo zikuwoneka ngati. Izo ndithudi zikutero. Nkulondola uko, mpingo? Kodi ilo silikuwoneka ngati guwa lakale lija? Chabwino, ine ndikuganiza Uthenga wakale womwe uja umene ife timalalikira kumeneko umadutsa pamenepo, mulimonse.

15 Kotero inu mukudziwa, alipo mkazi mmodzi yekha mu Baibulo yemwe anayamba wapentapo nkhope yake. Ndipo iye sanapente nkhope yake kuti akakomane ndi Mulungu. Iye anapenta nkhope yake kuti akakomane ndi mwamuna. Uko nkulondola. Inu mukudziwa chimene Mulungu anamuchitira iye? Anamudyetsa iye kwa agalu. Chotero pamene inu mumuwona mkazi atadzipenta, inu mungoti, "Mmawa wabwino, Abiti Nyama ya Garu." Ndizo ndendende zomwe izo ziri. Izo ndi zoipa, sichoncho izo? Koma ndicho chimene Mulungu amaganiza za zimenezo. Iye anangopangidwa nyama ya garu wamba ya agaru amtchire. Ndizo zomwe iye ali. Ena a ankhandwe olusa awa amene amapita kumeneko, akuimba muluzu, inu mukudziwa; chimene iwo amachitcha nkhandwe, inu mukudziwa. Ndicho chimene icho chiri, basi nyama ya galu kachiwiri.

16 Ndine wothokoza chifukwa cha akazi inu. Mulungu apereke chisomo kuti akugwireni inu pamaso pa mtanda, muchokeko ku zinthu izi za dziko lapansi. Kuwonjezera apo, ife tiri pa njira yathu tikupita ku Ulemelero. Ndife mzika za Ufumu wina.

17 Kalekale kwambiri . . . Ine ndinali kungoyang'ana pozungulira pa omvetsera kuti ndiwone ngati ine ndingawone mmodzi wa anthu, ndipo ndiwo ena a abwenzi athu achikuda, Achinegro. Inu mukudziwa, kalekale kwambiri, kumusi kuno Kummwera, iwo ankakonda kupanga akapolo mwa iwo. Tsopano, ndine Wakummwera. Ndipo pali chinthu chimodzi chimene ine ndikufuna kuti ndinene za iwo, ine ndikukhumba ine ndikanayankhula ndi Martin Luther King. Munthu ameneyo, pokhala Mkhristu, sakudziwa kuti iye akuwatsogolera anthu

ake mu msampha wa imfa, kumene kukakhale mamilioni a iwo ataphedwa. Mukuona? Iye akulakwitsa.

18 Ine ndimawakonda abale anga, abale anga achikuda. Ine sindikanakhala ndiri mu Afrika ndi kozungulira, ndikulalikira kwa iwo, ngati ndikanakhala kuti sindimawakonda iwo. Iwo ndi anthu a Mulungu, chimodzimodzi monga ife tiri. Koma ine sindimakhulupirira kuti . . . Munthu ameneyo, pansi pa izi, iye adzangopangitsa ambiri, ambiri, ambiri a iwo kuti aphedwe. Ndiye izo zidzayambitsa kuwukira kachiwiri, zomwe sizidzachoka konse mwa anthu kumusi kuno. Chotero iwo si akapolo. Iwo ali nawo ufulu wochuluka monga wina aliyenseyo. Iwo, ngati iwo akanakhala akapolo, ine ndikanakhala mbali imeneyo. Koma iwo si akapolo.

19 Zangokhala chomwecho chifukwa chakuti iwo akufuna kuti azipita ku sukulu. Iwo ali ndi masukulu. Asiyeni iwo azipita ku sukulu. Uko nkulondola.

20 Ndinali kumeneko, mukumukumbukira m'bale wachikulire wachikuda uja yemwe anaimirira, mmawa umenewo, mu chipolowe chija. Iye anawafunsa asirikali ngati iye akanakhoza kuyankhula. Iye anati, "Ine sindinayambe ndachitapo manyazi kuti ndine munthu wakuda. Wondipanga wanga anandipanga ine munthu wakuda. Koma mmawa uno, ine ndikuchita manyazi momwe mtundu wanga ukuchitira. Kodi anthu amenewo akuchita chiyani kwa ife? Angokhala abwino kwa ife."

21 "Mkazi wachizungu," anadzuka ndipo anati, "Ine sindikufuna kuti ana anga aziphunzitsidwa ndi mkazi wachizungu," anati, "chifukwa iwo . . . iye samakhala naye chi—chidwi, kukhala ndi chidwi ndi ana anga monga mkazi wachikuda amachitira ndi mtundu wanga womwe." Anati, "Apo, tayang'anani pa masukulu athu. Iwo ali ndi madziwe osambira. Iwo ali ndi masukulu abwinoko ndi chirichonse. Ndi chifukwa chiyani ife tikufuna kuti tizipita ku masukulu awo?" Uko nkulondola.

22 Ine ndikukhulupirira Mulungu ndi Mulungu wa—wa, chabwino, ine ndinganene kuti Iye ndi Mulungu wa kasinthasintha. Iye amapanga mapiri aakulu ndi mapiri aang'ono. Iye amapanga zipululu. Iye amapanga nkhalango. Iye amamupanga munthu wachizungu, munthu wakuda, munthu wofiira. Ife tisamakweranitse konse zimenezo. Izo zimadzakhala haibridi. Ndipo chirichonse cha haibridi sichingakhoze kudzibala chokha. Inu mukuwononga mtundu wa anthu. Pali zinthu zina zokhudza munthu wachikuda zomwe mzungu alibe ngakhale makhalidwe amenewo. Mzungu nthawizonse amakhala akutafula ndi kudandaula; munthu wachikuda amakhutitsidwa mu chikhalidwe chimene iye alimo, chotero iwo samazisowa zinthu zimenezo.

23 Koma mmbuyo mu nthawi ya ukapolo, iwo anali kugulitsa akapolo, anthu okhalapo, monga mdadada wogulitsira, monga momwe angagulitsire magalimoto ogwiritsidwa kale ntchito. Pamakhala wogula amabwera, kudutsa mdzikoli, ndipo iye amakhoza kuwagula iwo, ndi kumapita kukawagulitsa iwo ndi kupangira ndalama pa iwo, chimodzimodzi monga momwe inu mukanachitira pa galimoto yogwiritsidwa kale ntchito kapena chinachake.

24 Silinali konse dongosolo la Mulungu! Mulungu anamupanga munthu; munthu anapanga akapolo. Wina si woti azilamulira pa mzake. Ife tikuyenera kuti tizikhala limodzi mu umodzi ndi mtendere.

25 Ndipo munthu uyu anabwera ku munda wakale. Iye—iye amafuna . . . "Ndi akapolo angati amene inu muli nawo?"

Anati, "Handiredi kapena kupitirirapo."

26 Iye anali akuwayang'ana iwo, ndipo iye anapezeka kuti wazindikira, panali kapolo mmodzi pakati pa anthu amenewo . . .

27 Akapolowo amakhala achisoni. Mabunu aku Afrika anali atawagwira akapolowo, amawabweretsa iwo kuno ndi kudzawapanga, ndi kuwagulitsa iwo. Ndipo iwo ankadziwa kuti sadzabwerera konse ku dziko la kwawo. Iwo ankadziwa kuti iwo anali kuno kwa moyo wawo wonse. Iwo sadzawawonanso ana awo kachiwiri. Iwo sadzawawonanso konse abambo ndi amayi. Iwo anali kuno kwa nthawi zonse, ndipo iwo amakhala achisoni. Ndipo iwo amakhoza ngakhale kutenga zikwapu, ndi kumawakwapula iwo, kuti awapangitse iwo azigwira ntchito. Ndipo chotero iwo ankayenera kuti aziwapangitsa iwo azigwira ntchito, chifukwa iwo sankafuna kuti azigwira ntchito. Iwo onse amakhala atabalalika basi.

28 Wogula akapolo uyu anayang'ana cha kumeneko. Ndipo iye anapeza pakati pa akapolo awa, panali mnyamata mmodzi. Iwo samasowa kumukwapula iye; chifuwa mmwamba, chibwano mmwamba, amakhala ali pa ntchito. Ndipo wogulayo anati kwa mwini wa akapolowo, anati, "Ine ndikufuna kuti ndigule kapolo ameneyo."

Anati, "Iye si wamalonda."

Iye anati, "Iye akuwoneka kuti ndi wosiyana ndi akapolo enawo."

Anati, "Iye ali."

29 Anati, "Nchiyani chikupangitsa kusiyanako? Kodi iye ndi bwana wa ena onsewo?"

Iye anati, "Ayi, ayi. Iye ndi kapolo basi."

30 Anati, "Mwinamwake inu mumamudyetsa iye mosiyana ndi momwe inu mumachitira ndi ena onsewo."

31 Iye anati, “Ayi, iye amakadyera limodzi kumalo kodyerako ndi akapolo enawo.”

Anati, “Nchiyani chimamupangitsa iye kukhala wosiyana kwambiri?”

32 Iye anati, “Ine nthawizonse ndinkadabwa zimenezo, inemwini, kufikira nditadzafufuza. Uko ku dziko lakwawo, mu Afrika kumene iye amachokerako, abambo ake ndi mfumu ya fuko. Ndipo mosalabadira kumene iye ali, iye amadziwabe kuti iye ndi mwana wa mfumu, ndipo iye amachita monga mmodzi.”

33 Aleluya! Ngati iwe uli mwana wamkazi wa Mfumu, ndiye usamachite monga dziko. Ngati iwe uli mwana wa Mfumu, usamachite monga dziko. Ife tiri, ife timadziwa kuti ndife ana aamuna ndi aakazi a Mulungu. Ngakhale ife tiri kuno mdziko lakuda la imfa ndi chisoni, komabe ife timadziwa kumene chuma chathu chiri. Ndife ana aamuna ndi aakazi a Mfumu; osati mfumu, koma Amfumu. Tiyeni tizichita monga chomwecho.

34 Mphindi pang’ono zapitazo, chifukwa chimene ine ndinachedwa, mtsikana wamng’ono waku Ethiopia akukonza chipindacho, ndipo ine ndinazindikira iye anali akuchita chinachake. Ine ndimayesetsa kuti ndilembe mutu wina wa Lemba wa chinachake chimene ine ndimafuna kuti ndiyankhulepo. Sindimabera kudzayankhula basi kuti ndidzamvedwe; ine ndimabwera kudzanena chinachake chimene chiti chidzathandize mpingo, kuti chidzachite thandizo linalake. Ndiyeno ine ndikuwerenga, ndipo dona wamng’ono uyu anakhala ngati akungozungulirazungulira. Molunjika iye anati, “Kodi inu mungandikhulukire ine, bwana?”

Ndipo ine ndinati, “Inde, amayi.”

35 Ndipo iye anati, “Iwo akundiuza ine kuti inu ndi mwamuna amene anapeza chisomo pamaso pa Mulungu, kuti pamene inu mupempherera wodwala, kuti Mulungu amayankha pemphero lanu.”

36 Ine ndinati, “Iye samangoyankha langa lokha, koma Iye amamuyankha aliyense amene ati amukhulupirire Iye.”

37 Iye anati, “Ine ndikudwala, bwana. Kodi izo zingakhale kuphotchola ngati ine nditakufunsani inu kuti mundipempherere ine pang’ono?”

Ndinati, “Ayi nkomwe.”

38 Ine ndinakwera kufika kwa iye. Ine ndinapemphera chinachake chonga ichi. “Ambuye Yesu, zaka zambiri zapitazo, pamene Inu munali kukhukhuluza mtanda wakale wolimba pa phiri la mchenga, ndi kukhukhuluza apo mphondero za Magazi amene anali akutsikira pansi pa nsana Wanu. Thupi Lanu laling’ono, lofooka linafooka kwambiri mwakuti Inu munagwera pansi pa mtolowo. Panali mmodzi amene anayima pafupi, dzina lake anali Simoni, Wachikuda, iye ananyamula

mtanda ndipo anakuthandizani Inu kunyamula iwo. Apa pali mmodzi wa ana ake, mmawa uno, akudwala.” Pafupifupi nthawi imeneyo, izo zinachitika. Mukuona? Iye ndi Mulungu wa mtundu wonse wa anthu.

39 Tsopano, abwenzi, ndinu omvetsera abwino chotero. Ndipo ine pokhala ndabwera kuchokera ku minda, ya umishonare kunja uko, pamaso pa adierekezi ndi asing’anga, ndi zina zotero, musamaganize kuti iwo sakakutsutsani inu. Iwe umayenera kuti uzidziwa zomwe iwe ukuzinena pamene iwe wabwera pamaso pawo. Koma pansi pa zonga zimenezo, ndiyeno nkubwera kuno kumene moto wa pakhomo ukuyaka pakati pa Akhristu, ndi zina zotero, inu simukudziwa kuti ndi kupepukidwa kotani kuti munthu adzayima monga chonchi. Ine ndikukhumba kuti ine ndikanangokhala kumbuyo uko mwa omvetsera ndi kumawamvera abale odzozedwa abwino awa akulalikira Mawu, ndipo ine ndingakhoze kungokwezera manja anga mmwamba ndi kumalira, ndi kufuula, ndi kumapemphera. Ndipo ndicho—ndicho—ndicho chinthu bwanji chimene icho chiri, kutenthedwa ndi Moto. Ndi chinthu chodabwitsa chotero. Koma kawirikawiri . . .

40 Abale anga, ine ndiri nawo abale ambiri amene amandikonda ine, ndipo iwo amandifunsa ine kuti ndiyankhule. Ndipo chotero ine ndikudziwa, amene anayitanidwa ku utumiki wa Mfumu, ine ndiyenera kuti ndiyesetse kugwira ntchito mopambana momwe ine ndingathere, koma nthawizonse ndimachita izo mowonjeza pokhala motalikitsa kwambiri. Ndipo ine ndikudziwa inu mukudikirira chakudya chanu chamadzulo, mwakhala muli muno kuyambira eyiti koloko mmawa uno, kapena chinachake, mu gulu ili la anthu. Koma ine ndinaganiza kuti, ndibwere madzulo ano kudzayankhula ndi inu kwa nthawi yaifupi chabe, ine ndinalemba zolemba zina apa, ndi Malemba ena, zomwe ine ndikufuna kuti ndilozereko. Ndipo pochita izi, poganiza kuti inu muli naye munthu pano yemwe ali woyenera kwambiri, ndi kuitana kwa Mulungu, kuti atenge malo awa, kuposa ine. Koma zanga ndi pemphero kwa odwala, kuwona masomphenya, ndi zina zotero.

41 Ndipo ine ndinali kuyankhula ndi winawake maminiti pang’ono apitawo. Ngati mungayang’ane mu *Life* magazini, mwezi wathawu, inu mudzawona mmenemo . . . Ndipo inu muli nayo tepi imeneyo. Ine sindine wogulitsa matepi. Koma ngati inu munayamba mwakhulupirirapo Mawu amene ine ndimalalikira, ndipo inu mukhoza kukwanitsa izo, mudzatenge *Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri,* ndipo choyamba mudzatenge *Ndi Nthawi Yanji Ino, Mabwana?* Mudzamvetsere kwa izo zikuyankhulidwa, miyezi sikisi izo zisanachitike. Ndipo sayansi yadodometsedwa. Nditaima pansi pomwe izo zinali kuchitikira pamenepo. Ndipo ndinazinena izo, miyezi sikisi zisanachitike, momwe kuti padzakhala Angelo seveni mmawonekedwe a

kuwundana, ndi kudzawoneka ngati piramidi, adzafika pansi. Ndipo ine ndikanadzakhala nditaima kumpoto kwa Tucson, Arizona, ndipo padzakhala mkokomo umene udzagwedeze ngakhale miyala kuchokera kumapiri. M'bale Fred Sothmann wakhala apoyo, yemwe anali ataima ndi ife, ambiri a iwo, pamene izo zinkachitika.

42 Tsopano sayansi inajambula chithunzi cha Zimenezo, inu munachiwona Icho, chinapita pa Associated Press. Iwo samadziwa chimene Icho chinali. Pali Mtambo utapachikika, mailosi twente-sikisi mmwamba. Ndiwo mamailosi fifitini, kapena twente, pamwamba ngakhale kumene chinyontho chimakhalako. Iwo sakudziwa chimene izo zonse zikuchitika, ndipo iwo akuyesetsa kuti azifufuze Izo. Ndipo apo, pansi pomwe pa Icho, ine ndinali nditaimapo. Ndipo Angelo seveni amenewo akubangula maliwu awo, a Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri zimenezo, ataima pamenepo. Ndipo mboni, zitatu za ife, monga mboni ya zinthu zimene zinaloseredwa pa tepi, *Mabwana, Ndi Nthawi Yanji Ino?* Ndipo pamenepo tsopano iwo akuyesetsa kuti afufuze. Icho ndi chinsinsi kwa iwo.

Ena a iwo anati, "Pitani, pitani, bwanji inu simukupita kukakawauza iwo?"

43 Izo zikanakhala basi monga pamene Mngelo wa Ambuye anawonekera kuno ku Houston, Texas, mu Kuwala kumeneko. Ine ndinawauza anthuwo, "Moyo wanga wonse ine ndakuwona Kuwala kumeneko."

44 Mpingo ukudziwa zimenezo. Sayansi ikudziwa zimenezo. Ndizo, chirichonse chimayenera kuchitira umboni pamene Yesu Khristu akupanga kusuntha. Ndi izo pamenepo. Magazini, ngati inu mukufuna kuti muyang'ane mmenemo, ndi imene ili ndi Rockefeller ndi mkazi wake watsopano kumbuyo kwake. Ine ndikuganiza ndi zolembedwa za mu Meyi za *Life* magazine. Iye ndi Mulungu. Ife tikukhala mmasiku otsiriza.

45 Tsopano ine ndabwera mmawa uno kudzayesa kutenga zolemba pang'ono apa, ndi zinthu, kuti ndidzayankhule pa chinachake chimene chingawuthandize mpingo, chingathandizire abale otumikira awa, kuti ndiyike mapewa anga ku gudumu ndi amuna awa. Ndife abale, ndipo iwo amandibweretsa ine kuno chifukwa iwo amakhulupirira mu utumiki womwewo. Inu mwapulumutsidwa mu msonkhano uno, bwanji inu simukutenga umembala wanu ndi ina ya mipingo yabwino iyi kuno imene imakhulupirira utumiki wa mtundu uwu? Iwo—iwo amakhulupirira izo, iwo amayima kumbuyo kwa izo. Ndipo ine—ine ndabwera kuti ife tikhoze kuyala Lemba ndi kwa chinachake chimene chingakhoze kuwuthandiza mpingo.

46 Ndipo phunziro langa, monga, mmawa uno, ndi chikhalidwe chiti chimene ine ndikuganiza kuti mpingo wa Chipentekoste ulimo wa tsiku lino. Ndi mayimidwe otani ndi ora lanji ife

tikuyimamo, ndipo ndi kuthekera kotani? Tsopano ndiroleni ine ndibwereze izo kachiwiri. Kodi mpingo uli mu chikhalidwe chotani tsopano, ndipo ndi kuthekera kotani kumene kuli patsogolo pake?

47 Ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Lemba, kwa mutu, ndipo ine ndikufuna kuti ndiwerenge kuchokera mu Bukhu la Oweruza, mutu wa 16, ndime ya 27 ndi ya 28.

> Ndipo *nyumba ina*dzazidwa ndi *amuna ndi akazi; ndipo onse a ambuye a Afilisiti anali kumeneko; ndipo apo panali pa denga pafupifupi amuna firii sauzande ndi akazi,* ndipo *ndinawona pamene Samsoni anapanga masewero.*
>
> *Ndipo Samsoni anaitanira kwa* AMBUYE, *ndipo anati, O Ambuye* MULUNGU, *mundikumbukire ine, ine ndikukupemphani inu,. . .ndilimbikitseni ine, Ine ndikukupemphani inu, izi kamodzi kokha aka, O* AMBUYE, *kuti ine ndikhoze kukhala. . .ndiwabwezere kamodzi Afilisiti chifukwa cha maso anga awiri.*

48 Ine ndikufuna kuti nditenge phunziro kuchokera pamenepo, kuchokera pamenepo *O Ambuye, Kamodzi Kenanso Basi.* Ambuye adalitse kuwerenga kwa Mawu Ake.

49 Iwo ayenera kuti anali a—madzulo abwino, chinachake monga ife tikusangalala lero kuno ku mabwalo a msasa awa, kuno mu Hot Springs, Arkansas. Ndipo uko kunali chikondwerero chachikulu chikuchitika, koma chosiyana kwambiri kuposa chimene chikondwerero chikumachitika lero. Panali pafupifupi Afilisti firii sauzande akuyang'ana pansi kuchokera mmakonde, kwa awiri achirendo omwe analowa mu bwalo lalikululo, ndipo akazembe olemekezeka kwambiri ndi madona awo okongoletsedwa ndi miyala yamtengo wapatali anali onse atakhala pamalo awo.

50 Ndipo monga izo zinkakhalira nthawi imeneyo, apo panali, oh, chinachake chonga chibowa chimene chinali pamenepo, nyumbayo itakhala pamwamba pa mizati imene imatulukira panja, chinachake monga mwinamwake mtundu wamakono wa zomangamanga, arc-. . .zomangamanga. Ndipo Afilisti onse awa anasonkhana kumeneko, ndipo anali atadziyika okha pa chochitika chachikulu ichi. Ndipo iwo anali mu chikondwerero chachikulu ichi, ndipo maso onse anali atakhazikika pakati pa bwalo ili. Iwo ayenera kuti anaimirira, kuti apeze ku—kuyang'ana kwabwinoko pa chochitikacho chimene chinali pafupi kuti chichitike.

51 Ndipo tsopano pamene ife takhala pano madzulo ano, tiyeni tiwone ngati ife tingathe, ndi malingaliro olingalira, tidziyike tokha pamalo amenewo, kuti tiyang'ane pa chochitika ichi. Kodi ife tikuwona chiyani?

52 Akubwera, akusunthira pakatikati pa bwalolo, kunabwera kamnyamata kakang'ono, atagwirizira dzanja la munthu wakhungu, akupunthwa, akudzandima pamenepo. Iwo anali atakhala ndi ziwonetsero zambiri za nyani, ndi—ndi timatsenga pang'ono, ndi zina zotero; koma tsopano inali itafika nthawi ya chochitika chachikulu, chinthu chimene iwo anali akuchiyembekezera kwa nthawi yaitali, chochitika chachikulu cha tsikulo. Akalambulabwalo anali atachokapo, maholo amene ankaphokosera masana onse ndi maphokoso awuchidakhwa. Pakuti, iwo anali akukondwerera chigonjetso cha Dagoni, mulungu wawo wa nsomba, za likasa ndi lonjezo la Yehova.

53 Ndi mawonekedwe ochititsa manyazi bwanji, monga ife tingaganizire chinthu choterocho chikuchitika; za mulungu wa nsomba wa fuko lachikunja, akukondwerera chigonjetso pa antchito a Yehova, zonsezo chifukwa cha kulephera kwa munthu kuti achite zinthu zimene iye anali atadzozedweratu kuti adzachite. Ndipo apa panali achikunja, oledzera, odzibwekerera, akazi okongoletsedwa, nkhope zopentedwa, chikondwerero cha Hollywood chamakono, akumubweretsa wantchito wa Ambuye Mulungu, atamangidwa mu maunyolo, kwa chochitika chachikulu cha madzulo.

54 Mnyamatayo ayenera kuti amakhukhuluzika pamenepo, akupunthwa, pakubwera thunthu lalikulu ili la mnofu wa munthu, maso onse ali panja, tsitsi likulendewera pansi ku nsana kwake, atanjatidwa ndiponso womangidwa, kuti apange chikondwerero kwa oledzerawo, gulu lomenyana la osakhulupirira. Iye ayenera kuti anapunthwa pa nsanamira pomwe amakapangira zosangalatsa kuti ziyambirepo.

55 Pamene ine ndiganiza za zimenezo, ine ndimaganiza za mpingo umene unadzozedwa ndi Mulungu, kuti udzamuchitire chinachake Mulungu. Ndipo iwo unamulola mdani kuti asawawone Mawu a Mulungu wamoyo ndi Malamulo a Mulungu, ndi ku ntchito imene iwo unadzozedweratu ndi Mulungu kuti udzachite; basi kuti adzaseleulidwe mmalo obisalira a oledzera, a nkhope-zopentedwa, akazi okongoletsedwa ndi miyala yamtengo wapatali, ovala zazifupi, odula tsitsi, ndi amuna adziko lapansi. Mpingo umene umayenera kuti uziwala mu mphamvu ndi nyonga za Ambuye! Ndi chamanyazi bwanji!

56 Zinali zochititsa manyazi bwanji kwa Samson! Ndi chimango chake chonse chitapangidwa, chimenecho chinali nako kuthekera moposa, ndipo anali atatsimikizira kuti Mulungu amakhala nazo mphamvu Zake kudzera mu chimango chake. Ndipo katumba aliyense yemwe iye anali naye, anali akadali mu thupi lake, koma madalitso a Ambuye anali atamuchokera iye.

57 Ife tikhoza kukhala ndi chimango chathu chonse. Ife tikhoza

kukhala ndi miyambo yathu ya chipembedzo. Ife tikhoza kukhala ndi maina athu pa pepala ndi mmabuku. Koma ndikudabwa, lero, ngati mpingo wa Chipentekoste suli kuyima pa malo omwewo, ndi maso ake atakolowedwa kuchoka ku Mawu a Mulungu, ndi kwa cholinga chimene Yesu anafera, kuti ife limodzi tikhoza kuyanjana pozungulira Mawu ndi zinthu za Mulungu.

58 Anachititsidwa manyazi, iye anali, pakati pa nthawi imene iye anakhalako. Pamene ine ndikumuwona Samsoni atayima pamenepo, ndi chophiphiritsa, chophiphiritsa cha fuko lakugwa, lovunda mwakhalidwe, ndi mpingo wakugwa mwakhalidwe, woipitsidwa, chifukwa iye monse anaimira Israeli monga fuko, ndi mphamvu ya Mulungu, yomwe ili ya mpingo. Iwo ndithudi anali mawonekedwe omvetsa chisoni, pamene ife tikumuwona iye ataima pamenepo, kuwonjezera apo, kubwera kwake pamenepo, ndi mnyamata uyu akumutsogolera iye, ndipo wopanda maso.

59 Ngati mdani atangochititsa khungu maso ako kwa chinthu chenicheni cha Mulungu, iwe ungayende pamwamba pake pomwe ndipo osadziwa izo. Ziribe kanthu zomwe Mulungu akuchita, ndi kuzitsimikizira izo mwa Lemba Lake, ndi kuzitsimikizira izo mwa mphamvu Yake, ngati maso ako sanatsegulidwe ku zinthu za Mulungu, iwe udzayenda kumene pa izo mwakhungu monga iwe ungakhalire.

60 Ndipo apo iye wayima. Kotero iyo iyenera kuti inali nthawi yopambana, pamene asilikari oledzera awa ndi akazi, ali ndi magalasi awo omwera mdzanja mwawo. Ine ndikukhoza kuzimva izo zikuphokosera kudutsa mmaholowo, "Chotero uyu ndi Samsoni, munthu wamphamvu wa Mulungu, mwamuna wamphamvu zogonjetsa, wankhondo wamkulu," atayima mu chikhalidwe chimenecho. Ine ndikulingalira, akudutsa pa ankhondo amenewo pamene iwo anaima ndi manja awo atawakumbatira okondedwa awo amakono aku Hollywood, ndi zokometsera zawo zabwino kwambiri zikumveka, mamembala a mpingo wawukulu uwu wa Dagoni, ine ndikulingalira ena a iwo akanakhoza kukumbukira, kuti mwa dzina la Samsoni, dzina lake lomwe linawagwedeza iwo. Dzina lake lomwe limabweretsa—limabweretsa mantha pa iwo, pakuti iye anadzozedwa ndi Mulungu. Ambiri a iwo amakumbukira zimenezo.

61 Ambiri a asilikari amenewo ataima pamenepo, amakhoza kukumbukira za kumuwona iye ataima ali ndi fupa la chibwanu cha bulu mdzanja lake, Afilisti sauzande atafa atagona pamenepo. Izo zingachitike motani? Pamene fupa la chibwanu la bulu linagunda chimodzi cha zipewa zimenezo, pafupifupi inchi-ndi-theka kukandapala kwa mkuwa wolimba, bwanji, iwe ukamenya chisoti chimenecho ndi fupa la nsagwada ya bulu, nsagwada ya buluyo ingakhoze kuwuluka mpaka kudzakhala

zidutswa sauzande. Koma Samsoni, ali ndi mphamvu ya Mulungu pa iye, anawamenyera pansi Afilisiti chikwi, kuswa zishango zawo ndi kudzazigoneka izo pa . . . mapazi ake. Ine ndikuganiza kuti ambiri mwa ankhondo amenewo anali atathawa nthawi imeneyo, anaima kumbuyo uko ndipo amakumbukira. "Ndipo ameneyo ndi Samsoni?"

62 Iwo amakumbukira kuwona fupa la chibwanu mdzanja lake, ndipo akuti, "Ndani winanso akufuna zina za izi?" Iye anali munthu amene amakhoza kuyankhula. Iye anali munthu yemwe anali wodzozedwa ndi Mulungu. Mulungu analonjeza kuti adzamudalitsa iye. Iye anali mu mphamvu ya Yehova.

63 Oh, mosakaika alipo ambiri pano akhoza kukumbukira mmbuyo pamene mpingo unayima mu mphamvu za mtundu umenewo, koma tsopano zonsezo zinasweka. Mitundu yonse ya zipembedzo, chimodzi chikumenyana ndi chimzake. Misonkhano yakale ya mapemphero ausiku wonse siyikumvekanso. Misonkhano ya mu msewu inapita mwamtheradi. Iyo inatha. Komabe, ife tiri nacho chimango chathu, ife tiri nacho chikhungwacho, koma kodi Mulungu wa zozizwitsa ali kuti? Moona, ambiri amawakana Iwo, ngakhale kukana machiritso Auzimu, ambiri.

64 Pomwe pano mu chikhalidwe ichi, ine ndinali ndi—munthu wa mpingo, ndi mpingo waukulu, anati, ine ndinkafuna kuti nditenge mipando ina, kuti ndidzaike kuno mu Hot Springs, ku Armory pamene ine ndinali kuno, ine ndi M'bale Moore, ndipo munthu wa Chipentekoste anati, "Ine sindingaloleze nkomwe . . . " Iye sangandilole ine kuti nditenge mipandoyo. Iye anati, "Ine sindingamulole aliyense kuti akhalire mipando yanga, amene amakhulupirira mu machiritso Auzimu." Zimenezo si kuno kokha, ziripo konsekonse. Chavuta ndi chiyani? Kusankhana, chifukwa cha kuthandizira ndi mabungwe ena, kuyiwala kuti ndife anthu a Mulungu mwa Kubadwa. Samsoni anali ataiwala zimenezo, nayenso. Ine ndikukhoza kukumbukira . . .

65 Ine ndikuganiza, pamene iye anali atayima pamenepo, panali ena a iwo akukumbukira usiku uja ku Gaza, momwe kuti munthuyo anakhoza kunyamula zipata za Gaza, nkuziyika izo pa mapewa ake, pamene iwo ankayesera kumutchingira iye mkati.

66 Inu simungakhoze kukuika mu mpanda kudzoza kwa Mulungu. Palibe bungwe lingakhoze kukugwira iko. Mulungu amawapulumutsa iwo amene Iye wawaitana. "Onse amene Atate andipatsa Ine adzabwera."

67 Chabwino, iwo ankaganiza kuti iwo anali atamutchingira iye mkati, ndiye iye anatenga zipatazo ndipo anaziyika izo pa mapewa ake, ndipo anachokapo, anakwera pamwamba pa phiri ndipo anakakhala pansi. Zipata zazikulu za mkuwa zomwe

zikanalemera mpaka matani, ndipo a—munthu wamng'ono anazikoka izo pa miyala, anazipinda izo ndi kuzigoneka izo pa phewa lake, ndi kumayenda chokwera phiri ndi iwo, kuchokera kwa chirichonse chimene chinkaima mu njira ya Mulungu.

68 Ambiri a iwo amene anali mu malo oledzera amenewo amakhoza kukumbukira zimenezo za Samsoni. Koma vuto linali chiyani lero? Iye sanati. . . Apo panaima Samsoni, koma Mzimu wa Ambuye sunabwere pa iye kenanso. Iye anali asanadzozedwe. Iye anali atavulidwa mphamvu iyi, ndi mkazi yemwe anamunyengerera iye kuchoka ku Malamulo a Ambuye.

69 Ine ndikudabwa, lero, ngati icho sichiri chinachake chonga mipingo yathu. Mukuona? *Mkazi*, mu Baibulo, amaimira "mpingo." Ndipo ndikudabwa ngati ife sitinamvetsere ku kutsogolera kwa zipembedzo zina, tayesetsa kuwaphunzitsa atumiki athu mu—digirii ya Bachelor of Arts, kuti osonkhana athu azikhoza kunena kuti, "Abusa athu ali ndi B.A., D.D., kapena L.D." Ndikudabwa ngati ife sitinaphotchole kukhala ndi mkwiyo wolusa kwambiri, kuti tiyesere kumanga tchalitchi chimene chiri chabwinoko pang'ono kuposa Amethodisti kapena Apresbateria? Ife tingakhale abwinoko mu mishoni ina, ndi Mzimu wa Mulungu pa ife, kuposa momwe ife tingakhalire mu chikhalidwe ichi. Ndikudabwa ngati ife sitinatembenukire ndi kukokera kuchoka ku imodzi kupita ku imzake, kuyesetsa kuti tipangwe mabungwe athu akule? Ndipo ife tatero, tiri ndi chimango chachikulu, koma Mzimu wa Ambuye uli kuti?

70 Apo iye anaima, atavulidwa ndi mkazi. Ndi chiyani chimene chiyenera kuti chimadutsa mmalingaliro a munthu ameneyo pamene iye anaima pamenepo? Iye anali ndi nthawi yoti aziganizire izo mobwereza.

71 Ine ndikuyembekeza mpingo umapeza nthawi yochuluka chomwecho. Zomwe ziri zochuluka kwa inu, kuchulukirapo ka millioni kapena mdalitso wakuya wa Mulungu mmoyo wanu? Ife tafufuza. . .

72 Ndipo ndikhoza kukhala ndi zina zambiri zomwe ine ndazilemba apa, za ambuye awo ndi zomwe Samsoni anachita, zomwe iwo anali kuganiza.

73 Tsopano tiyeni tipite uko kwa Samsoni. Ndipo kodi inu mukuganiza kuti chinali chiyani chimadutsa mmalingaliro ake, za zigonjetso zambiri zimene iye anali nazo, zinthu zazikulu zambiri zimene iye anali atachita pamene Mzimu wa Ambuye unali pa iye? Koma iye anali kudziwa kuti iye anali ndi akatumba aliwonse, koma Mzimu wa Ambuye unali kusowa.

74 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, mpingo. Musadzayesere kujowina mpingo wotchuka kwambiri, gulu lodziwa kuyankhula kwambiri. Inu muzikhala ndi Khristu, kumene kuli Mzimu wa Ambuye.

75 Ndiye iye ayenera kuti anaganiza za zigonjetso zazikulu zimene Mulungu anamupatsa iye, ndi za nthawi zimene maso ake anali otseguka, kuti iye amakhoza kuwona malonjezo a Mulungu. Koma tsopano, pakuti iye wagwidwa mu chinthu ichi, maso ake akoloworedwa.

76 Anthu ochuluka kwambiri, lero, akugwidwa mu chinyengo cha ubongo, samaganizira nkomwe zoti afufuze Lemba, kuti awone ngati izo ziri zolondola kapena ayi. Ena amayesetsa kumanena kuti, "Izo sizimapanga kusiyana kulikonse."

77 Paulo, mu Machitidwe 19, anaganiza kuti izo zimapanga kusiyanitsa. Ndipo iye anati, "Ngati Mngelo wochokera Kumwamba adzalalikira chinthu china chirichonse, msiyeni iye akhale wotembereredwa." Mukuona? Mukuona? Izo zimapanga kusiyanitsa.

78 Tsopano ife tikumuwona Samsoni ataima pamenepo, momwe iye akuganizira za zinthu zimene iye anachitapo nthawiyina ndi Ufumu wa Mulungu. Ndi za momwe Mulungu . . . Iye anali atamulephera Mulungu, ndipo iye anali atawalephera anthu a Mulungu. Inde, bwana. Tsopano iye ndi wamndende wa fuko lomwelo limene Mulungu anamuukitsa iye kuti adzaliwononge.

79 Ine ndikufuna kuti ndiyende apa mwaulesi miniti. Pentekoste, inu mukudziwa ine ndimakukondani inu. Pamene ine ndinabwera kwa inu, Jack Moore, Richard T. Reed, M'bale G.H. Brown, M'bale Ben Pemberton, ndi munthu wina wopambana, kuti ndifufuze zinthu zimene inu munali nazo, izo zinawoneka kuti ife tinali ndi zofanana kwambiri mpaka ife tinali ngati magolovesi amene anakwana pa dzanja; ine ndikugwirizana bwino ndi inu. Pakuti Uthenga, osadziwa kuti kunali mpingo woterowo, umene ine ndimawukhulupirira, apa panali kale gulu la anthu kuti awulandire Iwo. Ine ndikadali M'bale Branham. Ine ndikadali m'bale wanu, ndipo ine ndimakukondani inu.

80 Koma kodi inu mukuzindikira, kuti chinthu chomwecho chimene Mulungu anakuukitsirani inu, inu mwadzipereka kwa icho? Mulungu anakutulutsani inu ku mabungwe amenewo, zaka zapitazo, kuti adzapange anthu kuchokera mwa inu, ndipo inu mwapotoloka ndipo mwadzachipanga bungwe chinthucho basi cha chimene Mulungu anakutulutsaniko inu kuti mudzachinyoze.

81 Ine ndikutsutsa munthu aliyense kuti andisonyeze ine malo aliwonse mu mbiriyakale, kuyambira pamene mpingo unadzakhala bungwe koyamba, umene unali mpingo wa Roma Katolika, ku Laodikaya, kapena Nicaea, kani, Roma, pamene mpingo wa Katolika unadzakhala bungwe ndi kupangidwa bungwe . . . Ndipo kodi unatero mpingo uliwonse wochokera kwa Martin Luther, mbali ino . . .

82 Pamene Mulungu anamupatsa Martin Luther vumbulutso la kulungamitsidwa, ndipo mwamsanga pamene Luther anapita, iwo anapanga bungwe kuchokera mwa iwo, ndipo iwo unagwa. Motsatira kunadzabwera Wesley, pambuyo pake, ndi Asbury, ndi ena otero, anachokapo; iwo anapanga bungwe kuchokera mwa iwo, ndipo iwo unagwa. Motsatira kunadzabwera Alexander Campbell, ndipo iwo anagwa, ndi bungwe. Motsatira kunadzabwera John Smith, wa Baptisti, ndipo iwo unadzagwa. Ndipo nthawi iliyonse imene munthu ayesetsa kuti apange bungwe chinachake, cha kachitidwe kopangidwa ndi munthu, icho chimagwa ndipo sichimawukanso kachiwiri. Palibepo mbiriyakale, paliponse, pamene mpingo uliwonse umene unayamba wapangapo bungwe, koma umene unagwa, ndipo aliyense anagwa, sanawukenso nkomwe kachiwiri.

83 Ana a Israeli, mwa choimira, anali woti azitsatira Lawi la Moto. Ndipo usiku uliwonse iwo ankayenera kukhala okonzeka, osati kuti apange bungwe ndi kukhala pansi apa, koma kuti aziyenda ndi Moto.

84 Ndicho chimene Mulungu akufuna kuti anthu Ake azichita, aziyenda ndi Mzimu, aziyenda ndi nthawi!

85 Inu mukuti, "Chabwino, M'bale Branham, ife takhala nayo mitundu yonse ya mvula, ndi mvula yamkati ndi mvula yakunja." Ndinu aluntha. Ine sindikusamala mtundu wa vumbulutso umene ilo liri, ndi momwe ilo likuwoneka labwino, ngati izo siziri molingana ndi Mawu a Mulungu, zisiyeni izo zokha. Ichi ndi choyang'anira podutsa mchipululu, Mawu a Ambuye.

86 Koma apa pakuima mpingo lero, mpingo wa Chipentekoste, mu pafupifupi mabungwe twente kapena sarte osiyanasiyana, aliyense kumamutcha mzake winayo, *ichi, icho*, ndi *chinacho*, "chisa cha khwangwala," ndi zina zotero. Ndi chamanyazi bwanji, pamene chinthu chomwecho chimene Mulungu anakuchotseraniko inu kuchoka ku zipembedzo zimenezo, inu munadzapotolokapo ndipo munadzachita chinthu chomwecho chimene iwo anachita. Ndizo ndendende zimene Samsoni anachita. Mulungu anamuukitsa Samsoni kuti awononge fukolo. Ndipo Mulungu anakudzutsirani inu kwa anthu, osati bungwe.

87 Koma pamene Mulungu anayamba ndi Israeli kuchokera . . . kuchokera ku Igupto, iwo anali kokha pafupifupi ulendo wa masiku teni kuchokera ku dziko lolonjezedwa, pafupifupi mamailosi forte. Koma iwo anakhala mu chipululu kwa zaka forte. Chifukwa chiyani? Chisomo chinali chitawapatsa iwo mwanawankhosa chifukwa cha machimo awo, mdulidwe wa chizindikiro, Lawi la Moto ngati mboni, Mose ngati mneneri. Chisomo chinali chitapereka chirichonse chimene iwo

ankachisowa, koma iwo ankafuna chinachake kuti azichita iwoeni.

88 Iwo ankadziwa mochepa, pamene Miriamu anali akuvina ndi nkhotcho, ndipo ana a Israeli akuvina ndi iye, ndipo Mose akuimba mu Mzimu, iwo anali masiku teni okha kukafika ku dziko lolonjezedwa. Iwo ankadziwa mochepa, zaka forte, ndipo matupi awo amakhoza kuvunda mchipululu. Nchiyani chinachita zimenezo? Israeli anapanga chigamulo chake chopupuluma chimene iye anayamba wapangapo, pamene iye anavomereza lamulo mmalo mwa chisomo, pamene iwo ankafuna kuti awapange ena mabishopu ndi chinachake cha iwo eni, chinachake chimene iwo ankayenera kuti azichita mwa icho. Mulungu anali pakati pawo, akuwatsogolera iwo.

89 Ndipo ndicho ndendende chimene Pentekoste inachita. Pamene Mulungu anawulula chinachake chatsopano mu Lemba, mmalo mwake iwo anachitcha icho zinthu zatsopano kapena chirichonse chimene inu mukufuna kuti muchite nazo izo. Koma pamene Mulungu anawulula chinachake, mmalo movomereza Choonadi ndi kuchiyesa Icho ndi Baibulo, iwo anatulukamo ndipo anadzapanga bungwe, anadzilekanitsa iwoeni. Ndiyeno potsatira panadza *ichi, icho,* ndi *chinacho*, ndipo tsopano inu mukuyima oyipitsidwa, mpingo wa Chipentekoste, wamangidwa mu zingwe za bungwe. Chinthu chimene Mulungu anakuukitsirani inu kuti muchiwononge, ndipo tsopano inu muli chabe bungwe chimodzimodzi monga iwo aliri. Amuna aumulungu mwa aliwonse a iwo, ndi akazi; izo nzoona, mmodzi aliyense wa iwo.

90 Ndipo ife tiri, mmodzi aliyense, wolakwa. M'phika sungakhoze kutcha ketulo kuda. Ndife tonse olakwa, mmodzi aliyense wa ife, inu aumodzi, auwiri, autatu, ndi—ndi chirichonse chimene inu mungakhale muli. Ndi chamanyazi bwanji! Ndi chitonzo bwanji chimene inu munachibweretsa pa Yesu Khristu! Ndi chitonzo bwanji kwa dzina la pentekoste! Iwo abweretsa chitonzo chochuluka kwambiri mpaka ilo lasanduka dzina lamanyazi, pafupifupi. Anthu sakufuna nkomwe kuti aziyanjanitse okha ndi dzina loterolo. Ndi chifukwa chakuti inu munachita zimene inu simumayenera kuti muchite. Ndi kumapitirira ndi kumatsatira malamulo a Ambuye, mumayenera kukhala gulu limodzi lalikulu la Mulungu, mukuguba chamtsogolo waku chigonjetso, lero.

91 Iye anamusiya mkazi kuti amunyengerere iye kuchoka ku Mawu a Mulungu, tsopano iye akuima akuchita machenjerero a mdierekezi. Uko nkulondola. Ndendende basi.

92 Chinthu chomwecho chikuchitika lero, mulole Yezebeli, "mayi wa timahule," Chivumbulutso 17 amanena kuti iye anali "mayi wa timahule," tsopano, ngati iye ali hule, uyo ndi—ameneyo ndi mkazi yemwe amakhala wosakhulupirika kwa

mwamuna wake. Iye amadzinenera kuti Khristu ndi Mwamuna wake, ndipo samakhala moyo ndi Lamulo Lake.

93 Ndipo kodi mipingo inayo ikuchita chiyani? Hule ndi chiyani? Ndi chinthu chomwe chomwecho monga chinacho. Ndi chiyani chimenecho? Uhule ku Mawu a Mulungu. Ndipo iye anali "mayi wa timahule." Ndipo kulola chiphunzitso cha Yezebeli chimenecho, ndi zina zotero, chifukwa gulu la munthu waluntha, amene akufuna kusonkhana pamodzi ndi kupanga bungwe chinachake kuti iwonso akhale ndi maina akuluakulu iwoeni. Ndipo apo payima mpingo, ubale wogawanika. Oh, mai! Ndi chamanyazi bwanji! Inu mukudziwa momwe izo zimayendera.

94 Ndi chinthu chowopsya bwanji, wakhungu mwauzimu. "Oh," inu mukuti, "chabwino, sindine wakhungu mwauzimu." Zochitika zimayankhula mokweza kuposa mawu; zimatsimikizira kuti ndinu wakhungu mwanjira yomwe inu mumapunthwira pa zinthu. Mukuona?

95 Tsopano, kumbukirani, tepi iyi ikupangidwa ndipo idzatumizidwa kuzungulira dziko lapansi. Mwaona, ndipo ine sikuti ndikuyankhula mochuluka kwambiri pomwe pano, koma izi zikupita pafupifupi ku mafuko seventini osiyanasiyana, uko ku nkhalango ndi kulikonseko.

96 Akhungu mwauzimu! Akhungu kwa chiyani? Mawu a Mulungu, choonadi cha Mulungu. Bungwe lanu sililola . . .

97 Atumiki abwino amene amabwera kwa ine, ndi kuti, "Ine ndikukhulupirira zimenezo kuti ndi Choonadi, M'bale Branham, koma ngati ine ndingalalikire Zimenezo . . ." Tsopano, ndi zimenezotu pamenepo. "Ngati ine nditakhulupirira Zimenezo, chabwino, anthu angati . . ."

98 Ine sindikusamala zimene anthu akunena, ine sindikusamala zimene bungwe likunena; ndi zimene Mulungu ananena kuti ndi Choonadi. Ndipo ngati icho chiri Choonadi cha Mulungu, Mulungu adzachiyikira kumbuyo icho. Inu mungayembekezere bwanji kuti mukhale ndi chikhulupiriro pamene inu muli ndi zikhumbo zolemekezana wina ndi mzake? Mwaona, izo zimachotsa chikhulupiriro kwa inu.

99 Anabwerera ku zipembedzo, Pentekoste imene inabadwa kuchokera ku chipembedzo. Pentekoste sinabadwire mu chipembedzo; iyo inabadwira *kunja* kwa chipembedzo. Ndipo kuchenjera kwa Satana kunakukokerani inu kubwereranso mu zimenezo, kumene inu munatulukako, "Monga nkhumba inapita ku matope ake, ndipo galu amapita ku matope ake." Tsopano tayang'anani pa iwo, ogonjetsedwa!

100 Ife timayenera kukhala tiri kale mu dziko lolonjezedwa. Yesu Khristu ayenera kukhala wolemekezedwa kwambiri pakati pathu, mpaka osakhala matenda aliwonse. Oh, izo zingakhale zaulemelero.

101 Sipayenera kukhala akazi odula tsitsi, atavala madiresi aafupi. Ndipo—ndipo sipayenera kukhala mwamuna amene wakwatira katatu kapena kanayi, madikoni mu mpingo wathu. Ndipo musandiuze ine kuti izo mulibemo mu Pentekoste; izo ndithudi ziripo. Koma ndi chifukwa cha kutchuka kwa pa gululo. Izo sizikuyenera kutero, koma izo zikumatero. Chifukwa chiyani? Chifukwa cha zikoka zachipembedzo, ndale, ndalama, mmalo mogwirizana ndi Mawu. Kumuchotsa m'bale wina wofunikira, ndi kumuyika winawake chifukwa iye ali ndi maimidwe otukuka aakulu mu tawoniyo.

102 Ine ndikufuna munthu yemwe ali ndi maimidwe otukuka mu Ulemelero. Ngati iye sakudziwa ma ABC ake, kodi izo zimapanga kusiyana kwanji? Kodi inu mukudziwa chimene ABC amaimira? Nthawizonse kukhulupirira Khristu. Uko nkulondola. Inu mumaphunzira zimenezo.

103 Munthu wina anabwera kwa ine, osati kale kwambiri, ndipo anati, "M'bale Branham," kwambiri. . . mmodzi wa atumiki odziwika bwino kwambiri a Chipentekoste mu dzikolo. Iye ananditengera ine mmwamba mu chipinda chake, iye anati, "Ine ndikufuna kuti ndikupempherereni inu."

Ine ndinati, "Ine sindikudwala."

Iye anati, "Ine—ine ndimakukondani inu."

Ine ndinati, "Inenso ndikumverera chimodzimodzi."

104 Iye anati, anandiuza ine, anati, "Bwanji inu osasiya zowawuza akazi amenewo zokhudza tsitsi lawo lometa ndi mtundu wonse uwu wa zinthu, ndi zokhudza mpingo?" Anati, "Imeneyo si ntchito yanu."

Ine ndinati, "Ndi yandani ndiye?"

105 Iye anati, "Izo zidzafika pochitika kuti inu simudzakhala ndi kalikonse koma mulu wa nsanamira zoti muzizilalikira."

106 Ine ndinati, "Ine kulibwino ndidzachite zimenezo ndi kumalalikira Choonadi, kuposa kumunyengerera mdierekezi." Mukuona? Mukuona?

107 Iye anati—anati—anati—anati, "M'bale Branham, kodi Mulungu sanakuitaneni inu kuti muzipempherera odwala?"

Ndipo ine ndinati, "Inde, bwana."

Iye anati, "Anthu amakukhulupiriranі inu kuti ndinu mneneri."

Ndipo ine ndinati, "Chabwino, zimenezo—zimenezo, ine sindinayambe ndanenapo zimenezo."

108 Iye anati, "Koma iwo amakukhulupirirani inu mwanjira imeneyo." Ndipo anati, "Ngati ndinu mneneri, bwanji inu simukutaya nthawi yanu kuti muziwaphunzitsa anthu momwe mphatso zauzimu, ndi momwe angachiritsire odwala, ndi—ndi momwe angamachitire izi, kupeza mphatso zauzimu

izi, ndi kuthandizira mpingo mmalo momaima mowirikiza, kumawakalipira akazi kumeneko, ndi kumamukalipira mwamunayo, ndi zinthu monga zimenezo?" Anati, "Chabwino, bwanji inu simukuwasiya iwo okha?" Anati, "Bwanji inu simukuwaphunzitsa iwo chinachake chachikulu kuposa tsitsi lometa ndi zinthu, ndi kuzisiya izo zokha?"

109 Ine ndinati, "Ine ndingawaphunzitse bwanji iwo algebra pamene iwo sakudziwa nkomwe ma ABC awo? Uko nkulondola. Asiyeni iwo aphunzire ma ABC awo poyamba."

110 Mtumiki wachikulire anapita ndipo anakalalikira kulungamitsidwa pa chitsitsimutso, usiku wachiwiri, usiku wachitatu, usiku wachinayi, usiku wachisanu. Madikoni anamuitanira iye panja, ndipo anati, "Abusa, kodi inu simukudziwa zochuluka kuposa ulaliki wa kulungamitsidwa?"

111 "Oh, ndithudi. Koma asiyeni iwo onse alungamitsidwe poyamba, ndipo zikatero ife tidzalalikira chinachakenso." Uko nkulondola.

112 Oh, ngati inu mutangobwerera ku maziko! Apo panaima Samsoni, atagonjetsedwa.

113 Tsopano taonani, ife tikhoza kukhala okongola, izo zikhoza kukhala chomwecho. Koma ziri ngati kuti ine ndinali kubwera chotsika msewu tsiku lina, ine ndinawona chikwangwani chachikulu, chinati, "chimanga cha haibridi, cha Funk," momwe icho chinali chabwino. Koma icho si chabwino. Icho si chabwino basi monga icho chingakhoze kukhalira, ndipo icho chikupha fuko. Inu mumawerenga za icho, Reader's Digest, "Ngati akazi azipitirira kumadya nyama ya haibridi ndi chimanga, ndi zinthu, iwo sadzakhala ndi mwana mu zaka twente kuchokera pano." Mulibemo chabwino mmenemo.

114 Kodi haibridi ndi chiyani, mbewu zochita kupanga? Ngati iyo si mbewu yapachiyambi, iwe umayenera kuti uziyipopera iyo nthawi zonse, kuti uchotse tizirombo pa iyo. Tizirombo tidzaidya iyo. Koma ngati iyo ili mbewu yapachiyambi, inu simumasowa kuyipopera iyo. Mbewu yabwino yathanzi, kachirombo sikangakwawire pa iyo.

115 Ndiro lomwe liri vuto, iwe umayenera kuti uziwapembedzera anthu mu mpingo, "Ulemelero kwa Mulungu, mlongo," mwaona. Ndinu wa haibridi, inu munabweretsedwa mwanjira ina.

116 Inu mutenge chimanga cha haibridi chimenecho ndi kuchibzala icho mobwereza, ndi chiyani inu muli nacho? Palibe. Icho sichidzapanga nkomwe kalikonse.

117 Mpingo ndi wokongola lero, izo nzoona, nyumba zazikulu kuposa zomwe inu munayamba mwakhalapo nazo, magulu aakulu amene inu munayamba mwawalalikirapo, atumiki abwino aluntha kuposa omwe inu munkakhala nawo. Inu

munkakhala ndi munthu wochokera mmunda wa chimanga kwinakwake, amene Mulungu anamuyitana kunja kumeneko pa kagawo ka thengo la tsache. Koma tsopano inu mwawatumiza ana anu ku sukulu, ndipo mwapanga zidzukulu kuchokera mwa iwo, ndipo abwererako ndi ma Ph.D, ndi LL.D. Ndipo ngakhale umodzi wa mipingo yaikulu ya Chipentekoste lero, iwo asanamutumize munthu ku minda ya umishonare, iye ayenera kuima pamaso pa wopima zamisala kuti awone ngati iye wasokonezeka mmaganizo mokwanira. Taganizani za zimenezo!

118 Mu Pentekosite, chofunikira sichinali kuyeza kwa mmaganizo, kunali kuyeza kwa Mzimu Woyera umene unagwa pansi pa Tsiku la Pentekoste. Izo ziri kunja kwa funso kwa anthu lero.

119 Kodi inu mumadziwa kuti mpingo wa Roma Katolika unali mpingo woyamba wa Chipentekoste wapachiyambi? Izo zinatengera iwo zaka thuu sauzande kuti ufike pachikhalidwe chimene iwo uli lero. Ngati bungwe la Chipentekoste ili lizingopitirira zaka zina fifite, ilo lidzakhala loipa kuposa mpingo wa Katolika. Uko nkulondola. Tchimo likuwunjikana kumbali iliyonse! Tsopano inu mukhoza kusaganiza kuti ine. . .Inu mukhoza kuganiza kuti ndine wopenga, koma ine ndikudziwa pamene ine ndiri. Mukuona? Ndipo izo nzoona. Inu mungodikira ndipo inu mudzazipeza. Inde.

120 Cha haibridi, chimanga cha haibridi, kuwapangitsa akazi kuti aziwonda mu ziwuno zawo ndipo kumakula mmapewa, ndi zina zotero.

121 Kusintha kumatiuza ife zimenezo, mu kusintha, kuti nyama zina zinabwera pamodzi ndipo zinabala chinachake chosiyana, ndi chinachake chosiyana, izo zinadzatulukira kwa munthu. Iwo anapitiriza kumafufuza mpaka iwo anadzatsutsa mfundo yawo yomwe.

122 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, inu alimi pano. Nchiyani chimapanga mphongolo? Iye ndi chinyama choipisitsa mdziko. Iye ndi haibridi. Iye alibe chokhudzira chirichonse, kuyamba ndi kuyamba. Sungakhoze kumuphunzitsa iye kanthu. Iye amadikirira moyo wake wonse, kufuna adzakukankhe iwe iye asanafe. Iwe sungakhoze kumuuza iye kanthu. Ndi chiyani chimenecho? Chifukwa iye ndi haibridi.

123 Zikungondikumbutsa ine za Akhristu ena a haibridi, otchedwa chomwecho. Inu mukhoza kuyesera kuyiwuza mphongolo yakale chinachake, iyo imaima ndi makutu ake mmwamba, nkumapita, “Hoo! Hoo! Hoo!” Mukuona? Zonse zimene iye amadziwa ndi kulira ndi kumapitirira. Inu simungakhoze kumuuza iye choonadi ndi kumuphunzitsa iye kalikonse. Ndi momwe anthu awa. Ukawauza iwo za Khristu, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse, “Hoo! Hoo! Masiku

a zozizwitsa anapita," kulira kwa seminare ina imene ife tinaphunzira. Ndi haibridi.

124 Mzimu Woyera udzavomereza lamulo lirilonse la Mulungu ndi "ameni." Umenewo ndi mzimu wa seminare-chinachake ukutuluka mwa iye. Osati kulira motsutsa Mawu a Mulungu, ngati iwo uli Mzimu Woyera. Iwo udzavomereza izo "ameni." Mukuona?

125 Inu mukudziwa, ine ndikuganiza mphongolo ndi umbuli. Koma inu mukudziwa chiyani? Iye sangakhoze kudziwa yemwe bambo ake anali kapena amayi ake anali. Mwaona, abambo ake anali jack wamng'ono, amayi ake anali kavalo, koma iye sangakhoze kuberekanso. Iye watha.

126 Chomera sichingakhoze kudzibereka chokha kachiwiri. Mudzatenge violet woyera ndi violet wa buluu, mudzatulutse violet wanu wa pinki; mudzabzale icho kawiri kapena katatu, icho chidzabwerera mwina choyera kapena pinki, mwaona.

127 Izo zikutsimikizira, mwaona, izo sazinabwere monga chomwecho. Mulungu anati, "Mulole chirichonse chibale monga mwa mbewu yake yomwe," ndipo umo ndi momwe izo zizikhalira. Munthu anapangidwa mu chifaniziro cha Mulungu, osati nyani. Mukuona? Zinthu zopenga zimenezo!

Zindikirani, inu mukudziwa, umbuli wa mphongolo. Koma inu mukudziwa chiyani? Inu simungakhoze kumuuza iye kalikonse. Iye ndi wouma mutu.

128 Koma ine ndikuganiza kavalo weniweni wa mtundu weniweni, oh, mai, iye amadziwa kuti amayi ake anali ndani, amene abambo ake anali. Iye ndi mbadwa. Iye amadziwa azigogo ake onse ndi chirichonse, chifukwa iye ndi weniweni.

129 Umo ndi momwe zimakhalira ndi Akhristu a haibridi awa, otchedwa Akhristu. "Masiku a zozizwitsa anapita. Chabwino, ife Apresbateria, ife Amethodisti, ife *akuti-ndi-akuti,* musamakhulupirire *Izi*. Ife Autatu, ife *chakuti-ndi-chakuti*, ife sitiri. Ife sitimachita *izi*." Mwaona, inu simukudziwa pamene inu mukuima.

130 Koma Mkhristu weniweni wobadwa mwatsopano weniweni wochokera mu Bukhu la Machitidwe, amadziwa ndendende pamene iye akuima. Iye amabadwa mwa Mzimu, ndipo *apa* pali weniweni wake. Iye amachokera ku nthambi ya Mulungu. Iye adzabala chinthu chomwecho nthawi iliyonse.

131 Nzosadabwitsa, mpingo ndi wokongola kwambiri. Koma chavuta ndi chiyani? Iwo ukuyenda wopanda Mzimu. Iwo wadzibala wokha, ndi dziko lapansi. Kuwalola akazi azivala zazifupi. Aziyimba limba, atapaka zophodaphoda. Kumulola mwamuna akwatire kaforo kapena kafaivi, ndi kumagwira malo awo, udindo. Mitundu yonse iyi ya zinthu zimene iwo akudutsamo, ndendende basi zimene Lemba linanena. Iwo ndi

wogonjetsedwa basi chimodzimodzi monga Samsoni anachitira. Ndendende basi. Inde, bwana.

132 Oh, monga Samsoni ankaganizira! Ine ndikhoza... Ine sindikufuna kukusungani inu motalika kwambiri; ine ndilumpha ina ya mitu iyi pano. Monga Samsoni ayenera kuti anayima pamenepo ndi kuganiza za kulakwitsa kwake, ndi kumene iye akanakhalako!

133 Kumbukirani Israeli. Kodi ine ndingakhoze, kodi inu mungandikhulululukire ine miniti, kuti ndibwerere ku Israeli? Kodi inu mukudziwa chiyani, kodi iwo anachita chiyani zaka forte zimenezo pamene iwo anapanga bungwe lawo kumeneko? Mmalo momapitirira kumapita, motsogozedwa ndi Lawi la Moto, Mngelo wa Ambuye, amene anali Khristu, mmalo momapitirira kumapita ndi kumamutsatira Iye, mu pafupifupi masiku teni iwo akanakhala ali mu lonjezo lathunthu, koma inu mukudziwa chiyani? "Iwo ankangoyendayenda mu chipululu," Baibulo linatero.

134 Iwo anafika ku Kadeshi-barnea, kumene kunali mpando wachiweruzo, ndipo kumeneko pamene azondi anabwerera ndipo anayankhula za dzikolo, iwo anati, "Ife sitingakhoze kuchita zimenezo."

135 Kalebu ndi Yoswa anati, "Ndife oposa kukwanitsa kuchita izo," pakuti iwo anali kuyang'ana ku lonjezo la Mulungu, osati chimene zochitikazo zinali.

136 "Ife sitingakhoze kukhala nawo mpingo wopanda kukhala nalo bungwe." Chabwino, inu simukuwona zimene Mulungu ananena. Uko nkulondola.

137 Kodi iwo anachita chiyani? Kodi Mulungu amawadalitsa iwo? Ndithudi, ndithudi. Iwo ankangoyendayenda. Iwo anakwatira akazi. Iwo analima minda ya mipesa. Ndipo iwo anakhala ndi ana, ndipo anachulukana. Ndipo iwo anachita bwino mu chipululu. Uko nkulondola. Komabe iwo sanali mu mdalitso wathunthu.

138 Chotero pamene onse awa amene anapanga gulu lalikulu ili la bungwe, "omenya akale" ilo linkatchedwa, chabwino, Mulungu anawasiya iwo kuti akhale kumeneko mpaka mmodzi aliyense wa iwo anafa. Ndipo zitatero Iye anayamba ndi m'badwo watsopano, pansi pa utsogoleri wa Yoswa, amene ankakhulupirira Mawu, ameni, ndipo iye anawatengera iwo ku dziko lolonjezedwa.

139 O Mulungu, mulole kam'badwo kakang'ono aka ka Achipentekoste kapeze—kapeze masomphenyawo. Mwaona, iwo anapitirira waku dziko lolonjezedwa. Ife tiyenera kukakhala kumene tingakhale ndi mitundu yonse ya mphatso za Mulungu.

140 Ife tinayankhula ndi malirime. Uko nkulondola. Izo nzabwino. Palibe chotsutsa izo. Mose anawoloka Nyanja

Yofiira; mdaniyo anaphedwa kumbuyo kwake. Ife—ife—ife tikuyamikira zimenezo. Koma izo siziri apobe zonse za izo.

141 Ndi moperewera bwanji momwe abambo anu ndi amayi anaganizira pamene iwo anali atayima kunja uko ndipo akuwombera mfuti kudzera mmazenera pa iwo, ndipo iwo akuvina mu Mzimu, kuti ana awo akanati adzabwere konse kwa izi! Koma izo zinatero.

142 Koma ulipo m'badwo watsopano umene ukubwerapo tsopano. Tsitsi la Samsoni lakula. Mukuona?

143 Penyani! Musadzamulole konse Delila adzakulowetseni inu nkomwe kubwerera mu chinachake chonga icho. Uh-huh. Muzikhala kutali ndi zimenezo. Ndicho chinthu chimene chinakutemberererani inu. Inu munauka kuti mudzachiweruze icho. Ndipo ine ndayesetsa mwakukhoza kwanga kuti ndichite izo, ngakhale ine ndaima ndekha. Koma ndayesetsa mwakukhoza kwanga kuti ndiyime ndi Malamulo a Mulungu. Ine ndikuwuwona mpingo ukuima pamenepo, utavulidwa mphamvu ya Mulungu, utavulidwa madalitso, kuvulidwa mphatso.

144 Ndipo Mulungu adzatsanulira mphatso Yake pansi. Iwo amati—iwo amati, "Kumeneko ndi kuwerenga maganizo, kuwerenga ubongo," pamene iwo amayenera kuti azikumbatira Izo. Mukuona? "Chabwino, iye ali uko kwa Aumodzi tsopano. Ayi, ndizo, izo zikhoza kukhala, pakuti, oh, iwo anali *ichi, icho,* kapena *chinacho*." Mukuona? Oh, ngati inu mukanangolidziwa tsiku lanu! Musalole Ilo likudutseni inu. Lino ndi ora, kulumikizana mwa Khristu. Zindikirani.

145 Samsoni ataima pamenepo, akuganiza za kulakwitsa kwake, zinthu zimene iye anali atazichita. Tsopano kodi inu mukuzindikira chimene chinamupangitsa iye kukhala mwanjira imeneyo? Mdani anamukolowola maso ake.

146 Ndipo ndicho chinthu choyambirira chimene bungwe liti lidzachite, lidzachotsa maso anu ku chiyanjano china chirichonse koma icho cha inu eni. Ameni. Ine ndikhoza kunena gulu lonse la zinthu apo pomwe, koma ine—ine sindichita zimenezo. Koma inu, ngati inu muli a malingaliro auzimu, inu mukudziwa chimene ine ndikuchikamba. Ilo lidzachotsa maso anu! Basi inuyo ndi gulu lanu; ngati ndinu wa Methodisti, ndinu wa Methodisti basi; ngati ndinu wa Baptisti, ndinu wa Baptisti basi. Ngati ndinu wa Presbateria, ndinu...Ngati ndinu wa Oneness, ngati ndinu wa Twoness, ngati ndinu wa Threeness, kapena ndi ochuluka bwanji iwo ali nawo, mwaona, ndinu basi wa zimenezo. "Ena onsewo si abwino."

147 Abaptisti anali ndi mbalume mmasiku a masiku oyambirira a Billy Graham, forte-..."Mu' 44, millioni enanso." Kodi inu munapeza chiyani? Gulu la osuta-ndudu, ojowina-mpingo achinyengo.

148 Pamene Billy, mwiniwake, pamene ine ndinali pa kadzutsa wake, iye anati, “Iwe ukudziwa lomwe liri vuto?” Anati, “Apa pali chitsanzo.” Iye anati, “Ine ndipita mkati . . . ” Anati, “Paulo Woyera anapita mu mzinda, iye anali ndi wotembenuka mmodzi. Ndipo iye anadzabwwererako, chaka kuchokera pamenepo,” ndipo anati, “wotembenuka mmodzi ameneyo anatulutsa sarte owonjezera.” Iye anati, “Ine ndimapita mu mzinda kwa masabata sikisi, ndi kukakhala ndi zigamulo sarte sauzande, ndipo ine ndikhoza kudzabwereranso mmiyezi sikisi ndipo osakhoza kupeza sarte.” [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

149 Chabwino, tsopano, ine ndinamuyamikira munthuyo chifukwa cha kulimbika kwake, koma ine ndikufuna kuti ndimufunse iye funso limodzi. “Ndani anawatenga otembenuka a Paulo? Ndi m’busa waulesi bwanji wa iye?” Chinali chiyani chimenecho? Paulo anakhala naye iye mpaka iye atadzakhala kwathunthu mwana wa Mulungu, wobadwa ndi Mzimu. Iye anamutengera iye kutali kwambiri mwa Khristu mpaka iye sankakhoza ngakhale kuyang’ana mmbuyo.

150 Iwo amangoyenda chokwera ndipo mwinamwake kujowina mpingo, kapena ngakhale kuyankhula ndi malirime. Ine ndimakhulupirira mu kuyankhula mmalirime. Ine ndimakhulupirira Mzimu Woyera umayankhula mmalirime. Koma ine ndikudziwa kuti onse amene amayankhula ndi malirime alibe Mzimu Woyera. Mukuona? Ine ndawawonapo asing’anga akuyankhula mmalirime, ndi kumwa magazi kuchokera mu chigaza cha munthu, ndi kuyitanira pa mdierekezi, kuyankhula mmalirime ndi kuwatanthauzira iwo. Zimenezo si zokwanira ayi. Ayi, ayi. Moyo wa Khristu mwa inu, chipatso chimadzichitira chokha umboni, ndi zimenezotu. Koma ife timakhazikika pa zimenezo, “Ngati munthu ayankhula ndi malirime, ndizo zonse, msiyeni iye abwere adzalowe.” Taonani zimene inu muli nazo lero. Mukuona? Izo nzoona, kuyankhula mmalirime, koma osati Choonadi chonse.

151 Monga bambo wachikuda akudya chidutswa cha vwende. Iye anati, “Inu mukuzikonda motani zimenezo, Mose?” Iye anati, “Izo zinali zabwino, bwana, koma ndithudi pali zochuluka zina za izo.”

152 Ngati ine ndingathe kuyankhula ndi malirime, ndithudi ziripo zinanso za Iwo. Mukuona? Koma kodi ife timachita chiyani? Chimodzimodzi monga Israeli, anakhazikika pa chinthu chimodzi chimenecho, ndipo anayenda mu chipululu tsopano kwa zaka forte, anali akadali opanda zina zonse Izo mdziko lolonjezedwa. Ndizo ndendende zomwe ife tachita.

153 Samsoni ataima pamenepo, (ine ndiyenera ndifulumire), ayenera kuti anayang’ana mmbuyo, ankaganiza za zinthu zonse zimenezo. Ndipo apa iye anali, chifukwa kumene chimene iye analeredwera, iye anachititsidwa khungu. Ndipo pamenepo

chimango chake chachikulu, bungwe lake lalikulu la thupi la munthu, phiri la mnofu litaima pamenepo, akatumba ake ojintcha kwambiri, koma opanda mphamvu.

154 Apa ife taima lero. Kumbuyo pamene Pentekosite inkakonda kuika paudindo ochuluka basi, mwinamwake anthu foro kapena faivi handiredi kudutsa fukoli, lero ndi mpingo umene ukukula kwambiri mdzikoli. Kodi ife tikulowetsamo chiyani? Gulu la mamembala. Ndi chimango chathu chachikulu, ife tiyenera kukhala olimba kuchulukitsa ka teni sauzande kuposa momwe ife tinaliri pamene ife tinkayamba. Ndipo ndife ofooka ka teni sauzande kuposa momwe ife tinali pamene ife tinkayamba, chifukwa ife tikuzimanga izo pa—maziko opandamalire, pa bungwe, chinachake chimene Mulungu wachitemberera. Ndipo ife tingamange bwanji a—mpingo pa moto wa Sodomu ndi Gomora?

155 Ine ndikuyembekeza inu simundida ine, koma inu mungokhala chete miniti ndi kumamvetsera. Mukuona?

156 Iye sangakhoze kuchita zimenezo. Chimene Mulungu wachitemberera, Iye wachitemberera. Ndiye, mundiyike ine kutali kwa chirichonse chimene Mulungu anachitemberera, ine ndikufuna chimene Iye akuchidalitsa. Uko nkulondola.

157 Zindikirani pamene iye anaima pamenepo, akuganiza. Magulu a nkhondo, ataledzera mwatheka, ataima pamenepo, "Ine ndikukumbukira munthu wamkulu uja. Ine ndikukumbukira pamene iye anaima ndi fupa la chibwanu cha—cha mphongolo, mdzanja lake. Ine ndikukumbukira pamene iye anapinda zipata za Gaza ndipo anayenda kukwera pamwamba pa phiri. Ine ndikukumbukira zinthu zonse izi. Pamene mkango umenewo unamubangulira iye, munthu wamng'ono kwambiri uja, ndipo Mzimu unabwera pa iye, ndipo iye anangowung'amba mkango umenewo pawiri, ndi dzanja lake. Ndipo apa iye wayima, atamangidwa, ndi mwana wamng'ono akumutsogolera iye pamenepo. Ndipo mulungu wathu, mulungu-wansomba Dagoni, wapambana chigonjetso pa iye."

158 Ndi zimenezotu pamenepo. Dziko lakwawira mu mpingo, lapambana chigonjetso. Ilo lawavula akazi athu. Ilo lidzayika chikhumbo mu mtima wa anthu kuti azikhala kunyumba ndi kumawonera televizioni mmalo mopita ku tchalitchi ndi msonkhano wa pemphero. Chikondi cha mdziko chakwawira mkati ndipo chawutenga mpingo wathu wa Chipentekoste paulendo wopita ku gehena.

159 Chokhumba ndi chikhulupiriro? Kumuyendetsa munthu kudutsa mu mzere wa pemphero ndipo kumulola iye awone chirichonse chimene chikuchitika; usiku wotsatira, apo iwo abwereranso kachiwiri. Mbewu ya Abrahamu? Chikhulupiriro palibepo pamenepo. Icho chiyenera kukhala pamenepo, koma icho palibepo. Pamene inu . . .

160 Mulungu anamuuza Abraham nthawiyina, ndipo zaka twente-faivi iye anayembekezera izo. Ziribe kanthu kuti zinabwerera mmbuyo chotani, ine ndikukhoza kumumva iye akunena kwa Sarah, "Pita kunja uko, ndiwe wa usinkhu wa zaka sikisite-faivi. Upite ukagule matewera ena, ndipo ukatenge mapini ena ndi kupanga tinsapato tina. Ife tikhala ndi mwana."

"Iwe ukudziwa bwanji kuti iwe ukhala naye iye?"

"Mulungu wanena chomwecho." Ndipo izo zinakhazikitsa zimenezo.

161 Choyamba, mukuona, iye anali pafupifupi zaka twente atadutsa kusintha kwa thupi. Iye anakhala naye iye kuyambira ali pafupifupi usinkhu wa zaka sikisitini, ngati mnyamata. Sizinapange kusiyanitsa kulikonse; sanayang'ane pa zimenezo; sanalabadire zimenezo. Iye ankalabadira zimene Mulungu ananena. Anadzilekanitsa yekha kwa kusakhulupirira konse, anapita ku chipululu.

162 Ndiro lomwe liri vuto lero. Inu mukufuna kudzipanga nokha ndi bungwe la kusakhulupirira, mmalo modzilekanitsa nokha ku zinthu za mdziko; inu mumafuna kuwona momwe mungafikire pafupi mpaka kumapeto kwa tchimo. Muziwona momwe mungakhalire kutali ndi ilo.

163 Koma apa iwo anali. Masiku sarte oyambirira kapena twente-eyiti anadutsa. Omvetsera osakanikirana tsopano, ndipo inu akuluakulu mukudziwa chimene ine ndikuchikamba. "Sarah, wokondedwa, iwe ukumverera bwanji?"

"Palibe kusiyanitsa nkomwe, Abraham."

"Ulemelero kwa Mulungu, ife tidzakhala naye iye, mulimonse."

"Iwe ukudziwa bwanji?"

"Mulungu wanena chomwecho."

164 Zaka teni zinadutsa. "Akuwasunga mapinifolo amenewo pamenepo, ndi mathewera onse."

165 Ena a abwenzi ake anabwera pafupi, "Abraham, atate wa mafuko, iwe uli ndi ana angati?"

166 "Ulemelero kwa Mulungu! Pa nthawi ino, palibe, koma ine ndikhala nawo iwo."

"Motani, iweyo? Bwanji, ndiwe wa usinkhu wa zaka nainte."

167 "Sizikupanga kusiyana kulikonse. Icho chidzakhala chozizwitsa chachikulu tsopano kuposa icho chikanakhala ngati icho chinachitika kumbuyo uko zaka twente zapitazo."

168 Koma, lero, "Ine ndinapempherereredwa usiku watha. Ine sindikumverera bwinoko mulimonse lero." Mbewu ya Abraham?

169 Chavuta ndi chiyani? Inu mwavulidwa. Minyewa yanu ya tchalitchi ikadali pamenepo; bungwe lanu ndi lalikulu

monga la Methodisti kapena la Baptisti. Inu mumakhala mukumanga minyewa iyi nthawi zonse, koma kodi chiri kuti chikhulupiriro chenicheni chija? Oh, inu mumawomba mmanja anu, inu mumafuula ndi kumaimba nyimbo, ndi kumavina. Mai, ine ndaziwona izo zikuchitika mwa madokotala ochuluka, misonkhano ya asing'anga, ndawawona iwo akuwomba manja awo, ndi kuyankhula mmalirime, kutanthauzira, ndi kumalumpha chokwera-ndi-chotsika. Atate Auzimu ali nacho chinthu chomwecho. Icho si chimene ine ndikuchikamba.

170 Ine ndikuyankhula za chikhulupiriro chenicheni chimene chingakhoze kufutukula lonjezo la Mulungu, ndi kuyima pamenepo ndi kuzipanga izo kukhala moyo, chinthu cha Mwamalemba.

171 Achimuhamadi, ine ndawawonapo iwo akugwera pa msewu ndi kumakuwa, "Allah, Allah, Allah" mpaka iwo kukhala ozindikira. . . Ine ndi Billy Paul tinayima pamenepo ndipo tinamuwona mwamuna akutenga lupanga ndi kudzibaya pansi pa mtima wake, ndipo dokotala kunatsanulira madzi kudzera mbali *iyi* ndi kukatulukira mbali inayo. Kumuwona iye akutenga ka—kachidutswa, nkondo ndi kuwuyendetsa iwo kudutsa pa mlomo wake ndi mmwamba kudutsa mphuno yake, ndipo osakhetsa ngakhale dontho. Kuyendetsa tomatuka pansi pa zikhadabo zake, akufuula, "Allah, Allah, Allah! Allah, Allah! Allah, Allah, Allah," monga chomwecho. Wachimuhamadi, ndi kumanyoza malingaliro a Yesu Khristu. Iye analibe Mzimu Woyera. Ayi, ayi, koma iye anali ndi kutengeka. Izo nzoona. Ndife . . .

172 Chikhristu kwenikweni si kutengeka. Chikunja chikhoza kubereka kuwerenga maganizo kochuluka basi monga—monga—monga Chikhristu chingachitire; koma izo si Choonadi. Ife tikufuna Choonadi. Khristu ndi Choonadi.

173 Kodi ife timachita chiyani? Ife tinadzikonza tokha kuti ife tiyime monga Samsoni, tsopano, pamene iye anaima pamenepo akuganiza chimene iye akanakhoza kukhala. Ine ndikuganiza, lero, mpingo uyenera kuyima ndi kuganiza limodzi nane, maminiti pang'ono, zomwe ife tikanakhala ngati zinthu izi zikanapanda kuchita izi. Zomwe ife tikanakhala!

174 Ndiye izo zikufika ku malingaliro ake, chinachake chinafika. Ine ndikukhulupirira Mulungu anachita zimenezo. Oh, ngati izo zikanakhoza kokha kuchitika pa bwalo la msasa ili! "Kulipo kuthekera." Kulipo kuthekera. Mulungu ndi wokhululuka. Kulipo kuthekera.

175 Ife tiribe nthawi yaitali kuti tikhale kuno. Nthawi yathu ikutha. Chitaganya cha mipingo chikulitenga dzikoli. Icho chidzalumikizana ndi Chikatolika. Ife tiri naye munthu mmenemo ndendende basi.

176 Ndikukhumba ndikanakhala nayo nthawi kuti ndipite mu zimenezo, kuti ndikusonyezeni inu kuti fuko lino liri chimodzimodzi basi monga Israeli. Iwo anabwera mu dziko lachirendo, anawathamangitsamo okhalamowo, ndipo anadzalitenga dzikolo. Ndicho chimene ife tinachita. Israeli, iwo anali naye munthu woyamba, munthu wamkulu, amuna otero monga Yoswa, amuna otero monga Davide, monga Solomoni; koma potsiriza apo panadzabwera munthu pa—pa ufumu, Ahabu, chigawenga. Ife tinali naye munthu wamkulu, Washington, Lincoln; koma tsopano chimene iwo anachita? Chinthu chomwecho chimene ife tinadzera kuno ufulu, inu mwakachiyika icho ku White House, chifukwa inu mukuganiza zochuluka za ndale zanu kuposa momwe inu mukuchitira za Khristu. Kulondola ndendende.

177 Ndipo kumbukirani, mu nthawi imeneyo, atumiki onse anagonjera. Yezebeli anali mtsogoleri. Mvetserani, Ahabu mwiniwake anali munthu wabwino kwambiri, koma Yezebeli ndiye anali yemwe ankalamulira. Iye anali mmodzi amene amachita zimenezo. Iye anali chigawenga. Ine ndiribe kanthu kotsutsa munthu ameneyo, ngati purezidenti, koma ndi kachitidwe ka Yezebeli ako kamene kali kumbuyo kwake. Kodi inu simukutha kuwona, mapapa awa ndi zinthu zikubweramo tsopano, wina akuuka yemwe "sakumudziwa Yosefe." Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, ife pakali pano tikupempha mpingo wa Chiprotestanti kuti ugwirizane nacho icho, ndipo bungwe lirilonse lidzapita mpaka mu chitaganya cha mipingo, ndipo apo inu mwagwidwa.

178 Ife tikukhala moyo pa ndalama za msonkho zomwe ziti zidzalipiridwe mu zaka forte kuchokera lero. Fuko lasweka. Kodi izo ziri kuti? Ndani ali ndi ndalama? Ife tiribe izo. Chathu—chuma chathu sichiri bwino. Ife tiyenera kukhala ndi golide. Ndani ali naye iye? Mpingo wa Katolika. Kodi iwo adzachita chiyani? Pamaso pa amuna a kachasu awa ndi onse akuluakulu ndi osunga masheya adzazisiya izo konse, iwo mwamtheradi adzagulitsa, ndipo mpingo udzabwereketsa fuko ndalamazo. Ndipo iwo udzachita chiyani, iwo udzagulitsa maufulu obadwa nawo ake molunjika kumene kukalowa mu Chikatolika. Ndiye inu mudzachita chiyani? Ameneyo ndi golide wa mdziko lapansi, iwo ndi Ayuda, ndipo limenelo ndi pangano limene iye akupanga ndi Israeli.

179 Mwaona, inu owerenga Baibulo mukakhoza kuphunzitsa zimenezo mu mpingo wanu. Inu mukuona, ine ndikungokuwonetsani inu kuti ine ndimakhulupirira chinthu chomwecho.

180 Ndi momwe izo ziti zidzachitikire, ndipo ife tiri nazo izo pomwe apo tsopano. Ndipo ndife pano, bungwe, ndi chilemba cha chirombo pa ife, ndendende basi monga chirombo choyamba; fano kwa icho, chitaganya cha mipingo, kujowina

mphamvu. Ndipo iwo anapanga fano kwa chirombo, kuti icho chizikhoza ziwiri zonse kuyankhula, ndipo icho chinachita chinthu chomwecho chimene chamoyo choyamba chinachita icho chisanakhalepo. Mu ndodo zathu zomwe! Oh, ana!

181 (Ndi nthawi yanji ino?) "Kodi ulipo mwayi?" Samsoni anaima pamenepo ndipo anati. . .(Ndi nthawi yanji?) Basi. . . "Kodi kulipo kuthekera?" Samsoni anapezeka akuganiza, "Mulungu wamkulu ameneyo! Iye ndi wopezeka ponseponse. Iye ndi Mulungu wosatha. Ine ndikuwona kulakwitsa kwanga. Ine ndilapa." Ndipo iye anafuula mokweza.

182 Ulipo mwayi kuti ifenso tikhoza kuchita chinthu chomwecho. Iwo a tsiku limenelo. . .Tsiku lino sakumawona masomphenya, monga Samsoni. Ngati ife tikanangowona masomphenya a mwayi! Yambani pomwe pano, pakali pano. Mwayi, mwaona.

183 Iwo anakhala mothinitsa, ndi kumawomba mmanja awo, ndi kumadabwa chimene icho chiti chidzakhale. Inu mudzapeza tsiku lina, inu mudzatulukira kumapeto aang'ono a nyanga, mwaona, nthawi imeneyo. Kukhala ndi kusonkhana kwakukulu, ndi kunyezimira, zinthu zachidziko, "Oh, ife tikuganiza, chabwino, inu mukudziwa chiyani? Ife tiri nawo mamembala ambiri kuposa omwe ife tinayamba takhalapo nawo. Ndipo ife tikhoza kumanga mabillioni a madola a nyumba, kukhala ndi ndalama zochuluka kuposa zomwe ife tinayamba takhalapo nazo, matchalitchi abwino mwinamwake kuposa ena a Achiprotestanti kapena ena a iwo omwe ali nawo. Oh, munthu! Maphunziro; chabwino, ife timawatengera ana athu ku sukulu, ndi kumanga maseminare atsopano kuti iwo azipitako."

184 Ndiroleni ine ndikuuzeni inu pakali pano. Mwamuna wokhala ndi maphunziro, wopanda Mzimu Woyera, amadzitengera yekha, akapeza digirii iliyonse, kutali kwambiri ndi Mulungu. Uko nkulondola. Inu mukuti, "Ine ndiri ndi Bachelor of Art." Ndiye kuti inu mwangokhala patali pang'ono kuposa momwe inu munaliri. Kugawa a—atomu, ndi kuphunthwa pa tsamba la udzu lomwe iwo sakudziwa kanthu za ilo. Inu munamvapo maneno akale, "Zitsiru zimayenda ndi nsapato zagogoda, kumene Angelo amawopa kupondako." Uko nkulondola, maphunziro, koma iwo samabweretsa Mzimu. Iwo samabweretsa ntchito ndi Moyo wa Yesu Khristu.

185 Vuto lake ndi lakuti, mpingo lero siuli monga Samsoni. Iwo sakulolera kulipira mtengo wake. Samsoni anapemphera pomwepo pamene iye anapemphera, "Ambuye, ndiloleni ine ndife ndi mdani." Iye ankadziwa kuti izo zikanamutengera iye chinachake. Iye ankadziwa kuti izo zitengera chinachake. Izo zikutengerani inu chinachake, izo zinditengera ine chinachake; kutchuka kwanu kwa azimzanu, malo anu ndi

udindo mu chipembedzo. "Ambuye, ndiloleni ine ndife, ndiye. Ine ndikuwona cholinga Chanu." Iye ankadziwa kuti icho chimutengera iye chinachake. Iwe umayenera kukhala wokonzeka kuti ufe, kwa mdani wako, kuti ulowe mmadalitso a Mulungu. Samson anali wololera kuti alipire mtengo, kuti apeze mphamvu ya Mulungu kachiwiri pa iye. Iye anali wololera kuti achite zimenezo. Ndi choncho inu?

186 Inu muli wololera kupereka maprogramu anu a pa televizioni? Ndipo, inu mukudziwa, izo zinkakhala zolakwika kuti ife tizipita ku makanema. Koma tsopano mdierekezi anaika imodzi pa inu, anayibweretsa iyo mnyumba momwe limodzi nanu. Uko nkulondola. Mukuona?

187 Ine ndinkakonda kupita uko kwa mlaliki wachikulire wa Methodisti, ndinkakonda kuyimba nyimbo:

> Ife talekerera zigwiriro, talekerera zigwiriro,
> Ife talinyengerera tchimo.
> Ife talekerera zigwiriro, nkhosa zatulukamo
> Koma mbuzi zinalowamo bwanji?

Inu munalekerera zigwiriro, ndizo zonse.

188 Oh, ine ndikumumva winawake akuti, "Tsopano dikirani miniti, M'bale Branham, ife tikumakhala nazo zitsitsimutso!" Eya, ndi chiyani chimenecho? Chitsitsimutso cha chipembedzo. Uko nkulondola. Tayang'anani pa makhalidwe anu ndi kutsemphana kwanu. Kodi icho ndi chitsitsimutso? Kodi ilipo nthawi yosweka? Kodi ilipo nthawi imene aliyense akhoza kuyanjana limodzi ndi kukhala ndi chiyanjano? Ngati bungwe lanu liri mmenemo, "izo zimakhala zabwino." Kumapita kutali kuchoka ku Mawu nthawi zonse, ndiko kulondola, kumapanga mabishopu atsopano ndi chirichonse. Mukuona?

189 Samsoni ankadziwa kuti chikhalidwe chake chobwerera mmbuyo cha nthawi imeneyo sichikanakhoza kubala mphamvu za chitsutso cha orali.

190 Amuna ndi akazi, abale anga ndi alongo, ndiloleni ine ndinene izi. Mpingo, mu chikhalidwe chake cha pano cha chipembedzo, sungakhoze kutulutsa mphamvu yotsutsa nthawiyi, kuyitcha iyo nthawi. Amuna ndi akazi akufuna Mulungu, mitima yoona. Ndipo inu mukhoza kuchoka ku—oneness ndi kupita ku twoness, inu mukhoza kuchoka ku twoness ndi kupita ku threeness, ndipo mukhoza kuchita zonse *izi, izo,* kapena *zinazo*; inu mukungokoka pepala, kapena—kapena kusinthasintha-matchalitchi, kapena kumachita ngati ine sindikudziwa chiyani, mwana wopanda khalidwe. Uko nkulondola. Inu simumazipeza izo monga chomwecho. Mphamvu zathu zobwerera mmbuyo, izo sizingakhoze kukumana ndi chitsutso cha ora lino. Zipembedzo sizingatenge kutsimikizira kwa Mawu.

191 Pamene, Yesu Khristu, monga ine ndimayesetsa kuti ndikuuzeni inu usiku wathawu, analonjeza izi mmasiku otsiriza. Iye analonjeza kudzakhala nazo izo apa. Ndipo inu mukudziwa izo, mwa Baibulo. Ndipo kwa zaka fifitini, mmbuyo ndi mtsogolo kudutsa fukoli, ndipo iwo akuipiraipirabe nthawi zonse. Uko nkulondola. Mwaona, iwo sakufuna zimenezo.

192 Iwo akumati, "Chabwino, tsopano, iye amayanjana ndi a oneness." Kapena, "Iye amayanjana ndi autatu. Iye amachita *izi, izo,* kapena *zinazo*." Ife timayanjana ndi Khristu, uko mu bungwe lirilonse, kuyesetsa . . .

193 Koma Mulungu amawonetsetsa kwa izo, kuti iwo awawone Iwo. Ndipo okhulupirira enieni amakhala ngati hule wamng'ono, usiku wathawu; mwamsanga pamene Iwo anawalira pa njira yake, ndipo mbewu ija ya Moyo itagona pamenepo, iye anakhulupirira Iwo. Izo zinali zonse, izo zinayatsa moto pakali pano. Pamene panali masauzande atayima pamenepo, akuwaseka Iwo, koma osati iye. Iye anadziwa kuti ameneyo anali Mesiya. Iye anadziwa kuti limenelo linali lonjezo, lakuti, pamene Iye adzabwera, Iye akanadzachita zimenezo.

194 Ndikudabwa, ngati ife tikanangodziwa chinthu chomwecho! Kodi ife takulungidwa kwambiri mu bungwe lathu, ife tikuletsedwa ngakhale kuti tiyang'ane pa Iwo? Ndikudabwa ngati inu mukuyang'ana pa m—magazini ndi zithunzi, ndi nyansi zauve zachikale za mdziko, mmalo mowerenga Baibulo lanu monga inu muyenera kumakhalira? "Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha, koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa mwa Mulungu."

195 Ana athu, anyamata athu, asanduka gulu la ma Ricky aang'ono ndi ma Ricketta, inu mukudziwa zimenezo nzoona, mulu wa magalimoto a mpikisano ndi chirichonse monga choncho. Ndipo pamene inu mumupeza mnyamata wa Chipentekoste? Ali ndi galimoto yake, pa msewu. Mlongo mukampeza kuti? Kumusi ku kantini kwinakwake, akupanga gwedemula. Kodi mukawapeza kuti abambo ndi amayi? Abambo, kumeneko akusewera gofu, kapena kunja kwinakwake monga choncho, ndipo amayi ali uko ku phwando lina la msuzi wa loji ina yomwe iye amapitako, kapena chinachake. Pamene, izo ziyenera kukhala kusonkhana limodzi mnyumba pansi pa utsogoleri wa Mzimu Woyera, ndi Baibulo litabwerereranso kachiwiri. Pamenepo ndi pamene ife tachokapo. Osati kukutsutsani, koma kungokugwedezani inu pang'ono, mwaona, kuti inu muthe kumvetsa.

196 Nthawi zonse, ndipo (oh, ine ndiyenera kuti nditseke) Afilisiti sanazindikire konse zomwe zinali kuchitika. Panali chinachake chikuchitika, chifukwa chinachake chinayamba kusuntha mu mtima wa Samsoni, "Apo panali kuthekera,"

mwaona. Iye anapapasa ku nsana kuti awone ngati izo zinali ziripobe.

197 Akazi ena akhalapo ndi nthawi yovuta tsopano, akudziwa kuti amayenera kukhala nalo ilo. Koma muwone ngati lonjezo Lake likadali pamenepo, muwone ngati Iye akupangabe... Mungomverera mmbuyo ndi kuwona ngati Iye sali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse.

198 Iye anamverera izo. Iye anadziwa kuti panali chinachake. Iye anadzutsa mutu wake. Iye analibe maso. Iwo sanazindikire misozi ikutsika kuchokera mmabowo opanda kanthu amenewo, pamene zosunga misozi zinali kugwetsera misozi pansi. Mutu wake mmwamba, milomo yake ikusuntha pang'onopang'ono, misonzi ikugwa kuchokera mmabowo ochititsidwa khungu amenewo. Iye anali akulapa. Iye ankadziwa kuti Yehova akadali moyo. Ngakhale iye anali atamulakwira, iye ankadziwa kuti Iye anali akadali Mulungu. Misonzi ikutsikira pa masaya ake, pamene iye anali atayima pamenepo. Afilisti anali ataledzera kwambiri kuti azindikire zimenezo.

199 Ngati mamembala a mpingo wanu, azimzanu mu mpingo sakuzindikira zimenezo, inu muzingopitirira kumapemphera. Iye ankafuna kuti awone, nthawi ina kenanso, Mawu a Mulungu akuwonetseredwa pamaso pa gulu la akhungu lija, oledzera a achikunja, osakhulupirira. Ngati imeneyo ili njala ya mpingo lero, kuti uwone kamodzi kenanso, chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale, chotumizidwa ndi Mulungu, kuchokera pa guwa mpaka kwa woyang'anira pano, kuyeretsa kwa kachitidwe-kachikale, chitsitsimutso cha kachitidwe-kachikale kokhala ndi mphamvu ya Mulungu, u—Uthenga umene umamuyeretsa munthu kwathunthu, kuchokera mkati mpaka kunja; mpope wa mfuti-utalunjika, kachitidwe-kachikale, mmbuyo-mkhalango, mlengalenga mwa buluu, kupha, chipembedzo chakupha tchimo chimene chimatenga Hollywood yonse kuyichotsa mwa inu, iwo amene ali ndi chidwi.

200 Apo iye anali, akupemphera. Osati chipembedzo chatsopano tsopano, kachikhulupiriro katsopano; koma kutsimikizira kwa Mawu. "Ambuye, Inu nthawiyina munali pa ine, Inu nthawiyina munandipatsa ine mphamvu. Ngati ine ndikanangokhala nayo mphamvu imeneyo! Ine ndiri nawo akatumba, koma iwo ndi ofooka."

201 Ife tiri nawo mamembala, koma iwo ndi ofooka. Iwo amakonda zinthu za mdziko mwabwino kuposa momwe iwo amachitira zinthu...Inu mukuti ndine zonse...Oh? Tayang'anani pa matchalitchi ndipo mufufuze. Musamayesere kuzikana izo. Zochita zanu zimayankhula mochuluka kuposa momwe mawu anu amachitira, mwaona. Oh, eya, ali ndi mamembala ambiri, akatumba aakulu, koma ilikuti mphamvu ya Ambuye? Akatumba anu aakulu sadzakumana ndi chitsutso

cha ora lino, chikhulupiriro chokwatulitsa kuwuchotsa Mpingo mu chinthu ichi chiweruzo chisanakanthe dziko lapansi.

202 Ndipo chiweruzo chikukonzekera kuti chikanthe. Ine ndinena, monga mzanga Jack Moore ananenera; ngati Mulungu amusiya Amereka kumapitirira ndi zinthu zimene iye akuchita tsopano, Iye adzakhala wokakamizidwa mwamakhalidwe kuti amudzutse Sodomu ndi Gomora ndi kumupepesa iye, chifukwa chomuwotcha iye. Kulondola! Chiweruzo chikutsatira.

203 Mulungu, chotsani chidziko chonse mwa ine. Ndipatseni ine chikhulupiriro, O Ambuye, cha Mkwatulo. Pakuti, padzakhala awiri pa bedi, ndipo mmodzi adzatengedwa, mmodzi adzasiyidwa. Awiri adzakhala mu—mu mpando wa galimoto, ndipo mmodzi adzatengedwa ndipo winayo adzasiyidwa. Izo zidzachitika mu kamphindi.

Inu mukuti, "M'bale Branham, izo zidzakhala liti?"

204 Inu mukhoza kutsutsa izi. (Ngati izo ziri zabwino kuti ndinene zimenezo?) [M'bale akuti, "Pitirirani ndipo nenani zimenezo, m'bale."—Mkonzi]. Ndiroleni ine ndigwetsere chinachake chaching'ono apa. Tsiku lina inu mudzapeza!

205 Inu mudzanena pamenepo, "Oh, ine ndinaphunzitsidwa kuti padzakhala *izi, izo,* ndi *zinazo*, zidzachitike Ambuye asanabwere. Padzakhala nthawi ya chisautso chachikulu, ndipo ife tidzadutsa mu zimenezo." Mukuona? Mukuona?

206 Inu mukudziwa, nthawi ina Yesu anafunsidwa funso. Iye anati, "Nchifukwa chiyani alembi amanena kuti Eliya ayenera kubwera poyamba?"

207 Ndipo Yesu anati, "Ine ndinena ndi inu, iye anabwera kale, ndipo inu simunadziwe izo."

208 Limodzi la masiku awa inu mudzanena, "Chabwino, ine ndimaganiza kuti Mpingo unali woti, unkayenera udzachite *ichi*, *icho*, ndi *chinacho*. Ine ndimaganiza kuti pakanadzakhala Mkwatulo. Ine ndimaganiza . . . "

209 Mwaona, uko kudzakhala kutengedwera kutali kwachinsinsi. Ngati Iye atatenga mmodzi kuno mu Hot Springs, ndi mmodzi kwinakwakenso, ndi wina kumusi uko, ndi wina kumeneko, zidzapanga mamillioni kwenikweni a iwo amene adzatuluke kuchokera mu nthaka. Ndipo pakumakhala pafupifupi anthu faivi handiredi, tsiku lirilonse, akusowa mdziko, ndipo ife sitikudziwa nkomwe kumene iwo akupita. Mwaona, Mkwatulo udzapangidwa ndi onse amene akugona mu fumbi la dziko lapansi, amene akuyanjana ndi Mulungu.

Iwo adzati, "Chabwino, ine ndimaganiza kuti Mkwatulo umayenera kuchitika."

"Iwo unadutsa kale, ndipo inu simunazidziwe izo ayi. Inu mwasiyidwa." Mukuona?

"Chabwino, chirichonse chikupita . . ." Inde, bwana.

210 Ndi Kudza kwachinsinsi, Mkwatulo uli, umabwera kudzababapo. Monga bukhu lija limene ine ndinawerenga nthawi imeneyo (linali chiyani ilo), Juliet ndi Romeo. Iye anabwera nthawi ya usiku, pamene anthu anali akugona mu chidziko, ndipo mpingo onse mu chidziko. Ndipo zonse mwadzidzidzi, kulira kunabwera, ndipo kutali iwo anapita.

211 Mvetserani, inu mwamva zochuluka kwambiri mwa Amuna Amalonda Achikhristu, Amuna a Full Gospel, akuti, "Oh, inu mukudziwa, M'busa Atate Woyera *Wakuti-ndi-wakuti*! Apresbateria ayamba kulandira Mzimu Woyera. Achilutera akuyamba kulandira Mzimu Woyera."

212 Inu gulu logona la anthu! Kodi inu simukudziwa Yesu anati, "Pamene namwali wogona uja anabwera kuti adzagule Mafuta, inali nthawi yomweyo imene Mkwati anabwera, ndipo iye analowa mkati"? Kumbukirani, iwo sanawapeze Iwo! Ndi kulondola uko? Monga Booth-Clibborn anati, "Huh?" Uh-huh. Iwo mwinamwake, anadutsa mu zotengeka zina, koma iwo kwenikweni sanawapeze Iwo. Pamene iwo anabwera kuti adzagule Mafuta, izo zinali nthawi itatha.

213 Ndipo apa iwo ali tsopano, a Presbateria, a Lutheran; tayang'anani pa a Full Gospel Business Men's *Voice*, ndipo gulu lija la zidzukulu za Chipentekoste ndi abale achipembedzo awa, kumaganiza kuti icho ndi chinachake chachikulu. Inu mukhoza kudzafunsa tsiku lina, "Chabwino, ine ndimaganiza *izi*."

214 "Izo zadutsa kale, ndipo inu simunazidziwe izo ayi." Mundirole ine ndiyimire pamenepo, chifukwa ine—ine sindiri pano kuti ndilalikire chiphunzitso.

215 Koma, kuthekera! Inu musawutaye mwayi umenewo. Tsiku lake ndi lino. Ora lake ndi lino. Kulipo kuthekera pakali pano, mwinamwake osati pa faivi koloko. Kulipo kuthekera. "Ambuye, ine ndikudziwa Ndinu Mulungu. Ine ndikudziwa Inu muli. Ine ndiri kutali ndi Inu. Koma ine ndikudziwa kuti minyewa iyi ya ine nthawi ina inanjenjemera ndi mphamvu ya Mulungu. Ine ndikudziwa zinthu zimene ndikuzisamalira lero, ine ndimadzinenera kuti ndine wa Chipentekoste;" akazi, "Ine ndimadula tsitsi langa;" abambo, "Ine ndimachita *izi, izo,* kapena *zinazo*."

216 Ndipo mwamuna iwe amene mumawalola akazi anu kumavala akabudula amenewo ndi kumachita zinthu zimenezo, ndiyeno nkumadzitcha nokha mwana wa Mulungu, manyazi pa inu.

217 Ine ndinapita ku mpingo winawake wawukulu wa chipembedzo, osati kale kwambiri, kwa . . . Iwo anali ndi msonkhano, ndipo ine ndinapita kuti ndikawachezere iwo. Ndipo abusa ananditengera ine kumeneko, ndipo iwo anali akuti akandisonyeze ine kwa akazi awo. Iye anali wa limba.

Ndipo mkazi ameneyo anali atavala diresi yothina kwambiri mwakuti khungu linali pafupifupi panja. Iye anali atazipenta, ndipo atavala mitundu yonse ya zinthu mmakutu mwake.

218 Ndipo ine ndinati, "M'bale, kodi inu mukutanthauza kunena kuti wanu—mkazi wanu ndi woyera?"

Anati, "Inde, bwana."

219 Ine ndinati, "Iye akuwoneka ngati wachikunja." Ine ndinati, "Ine sindinayambe ndawonapo zoterozo mu dzina la Pentekoste ndi chiyero!"

220 Oh, m'bale, ife tikusowa kuyeretsanyumba, kuchokera pa guwa kupita ku chipinda cha kupansi. Ndipo limodzi la masiku awa. . . Inu mukuti, "Ndine wa Chipentekoste." Izo sizikutanthauza mochuluka kuposa kukhala nkhumba, kwa Mulungu. Izo ziribe kanthu kochita ndi Khristu. Ilo ndi dzina chabe. Inu muyenera kukhala Pentekoste mu mtima mwanu, zipatso za Mzimu. Zindikirani. Oh, mai!

221 Iye ankadziwa zomwe zikanati zichitike ngati Mulungu akanayankha pemphero lake.

222 Kodi inu mukudziwa? Kodi inu mukudziwa kuti bungwe likuchotsani inu? Kodi inu mukuzindikira kuti inu mukupita pakali pano ku chitaganya cha mipingo, ndi zinthu zimene inu mukulowamo kumene? Kodi inu mukuzindikira mtengo umene inu mudzalipire? Inu mukuwadziwa akazi awo amene inu mumasewera nawo makadi adzakutchani inu "wakachitidwe kachikale" ndi mtundu wonse wa zinthu umenewo? Chifukwa inu simuwalola ana anu kuti azivala akabudula, ndipo inu mukuchita zinthu izi, inu mukudziwa mtengo umene inu mulipire? Inu kulibwino muziwerengere izo inu musanayambepo, mwaona. Inu kulibwino muziganizire izo. Eya. Inu kulibwino—inu kulibwino muziyankhule izo ndi Mulungu, poyamba, inu musanapange poyambira.

223 Iye ankadziwa, ngati pemphero lake linayankhidwa; koma iye anali wokonzeka, ndipo iye anali wodzipereka.

224 Ngati mpingo ungakhoze kokha kulowa mu chikhalidwe chimenecho! Ngati inu mwakonzeka pakali pano, ngati inu muli woonamtima, ngati inu mukutanthauza kwenikweni zimenezo, ngati maso anu atseguka ku zimene ine ndikuyesetsa kuti ndikuuzeni inu mwanjira yozungulira! Ngati ndinu woonamtima, ndiye munene kuti, "Ambuye, ine sindikusamala chomwe icho chiri, ndine wokonzeka. Ine ndikuwona chizindikiro. Ine ndikudziwa kuti nthawi yatha kuposa momwe ife tikuganizira. Ndi nthawi yoti tizibwera."

225 Ndiye Samsoni anafuula mokweza, "Ambuye, iwo anakolowola maso anga. Ine ndikudziwa kuti Inu ndinu Mulungu. Ine ndikudziwa kuti Inu muli nayo mphamvu yochitira izo. Ine ndikudziwa Inu mukhoza kundimasula

ine kuchoka ku zingwe izi. Kamodzi kenanso basi, Ambuye, kamodzi kenanso basi!"

226 Kamodzi kenanso basi, Ambuye, kamodzi kenanso basi! Mulole pakhale msonkhano wa msasa kumbali ya phiri, monga unachitikira pa phiri pa chipinda chapamwamba, mulole pabwere mkokomo wochokera Kumwamba, ngati mphepo yamkokomo, mudzaze nyumba yonse, umboni wowoneka wa Khristu wowukitsidwa.

227 "Kamodzi kenanso basi, Ambuye, kamodzi kenanso basi," iye anafuula. Pamene iye anafuula mokweza, moonamtima, atayima pamenepo, ndi maso ake akhungu. "Ine ndikudziwa mtengo, Ambuye, koma kamodzi kenanso basi!"

228 Mulungu amayankha pemphero. Iye anamverera minyewa ikumangitsa. Akatumba ake anayamba kugwira. Mphamvu ya mwendo wake inayamba kubwerera. Iye anati kwa mnyamata wamng'onoyo, "Nditsogolereni ine ku nsanamira tsopano."

229 "Nditsogolereni ine, Ambuye, nditsogolereni ine. Nditsogolereni ine ku nsanamira, ku Kalvare. Nditsogolereni ine ku nsanamira kumene ndingakapachikidweko, kufikira moyo wanga wakale wa chidziko utafera apa, ndi zonse zimene ine ndiri. Nditsogolereni ine ku nsanamira, Ambuye."

230 Pamene iye anayamba kumverera akatumba amenewo akumangitsa ndi mphamvu ya Mulungu, iye sankasowa kuti awone zomwe zinali kuchitika, iye ankamverera zomwe zinali kuchitika. Iye anayamba kupotokola mapewa ake, ndipo, pamene iye anatero, nyumbayo imapita ikugwa. Tsiku limenelo, iye anagonjetsa, iye anapha Afilisti ochuluka kuposa momwe iye anachitira masiku onse a moyo wake.

231 Abwenzi, kulipo kuthekera kumene mpingo uno, mu chikhalidwe ichi . . . Tsopano ine ndiri ndi pafupifupi masamba atatu kapena foro a zolemba pamenepo, ine ndizisiya izo zipite. Kulipo kuthekera. Kulipo kuthekera pomwe pano mu msonkhano wa msasa uwu. Kulipo kuthekera pomwe pano pa ora lino. Kulipo kuthekera, ngati ife tiri okonzeka kulipira mtengo wake, ife tikhoza kuwona Machitidwe 2 ena akuchitika.

232 "Kamodzi kenanso, Ambuye! Ife tasokoneza izo. Ife tapanga bungwe. Ife taphwasula ubale wathu. Ife talekanitsa chiyanjano chathu. Ife tatenga gulu laling'ono *apa*. Ife tikumenyana wina ndi mzake, ndipo mdierekezi wakhala kumbuyo uko, akutipenya ife tikukwapulana wina ndi mzake. Ambuye, kodi ndi zotheka kuti kamodzi kenanso kuti handiredi ndi twente a ife tikhoza kukhala mu mgwirizano umodzi pa malo amodzi? Kodi ndi zotheka kuti pabwere phokoso lochokera Kumwamba, ngati mphepo ya nkokomo wamphamvu? Kamodzi kenanso, Ambuye, kamodzi kenanso!"

233 Tiyeni tiyimirire pa mapazi athu, ndi kunena, "Kamodzi kenanso, Ambuye! Kamodzi kenanso, Ambuye!"

234 O Ambuye Mulungu, ndimvereni ine, Ambuye. Kamodzi kenanso, Ambuye! Kamodzi kenanso tumizani Mzimu pa msonkhano wa msasa uno, mu mphamvu ndi ulemelero!

63-0628M O Ambuye, Kamodzi Kenanso Basi
Associated Brotherhood Of Christians Campground
Hot Springs, Arkansas U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org